

# KUWERENGA CHOTSITSA



Zikomo inu, M'bale Neville. Ambuye akudalitseni inu.

Izo nthawizonse ndimakhala ngati ndimakhala paliwiwo. Ine ndangolowa kumene. M'bale Moore anali ndi ine pa foni za kupita kumusi kumeneko ku chisangalalo cha Chipentekoste cha zaka fifite. Ine ndinkayesera kupanga masiku ndi Amuna Amalonda uko ku malo ena, ndipo ine ndinati... ndinanyamula foni, ndinati, "Iwe ukumva 'Kungo Khulupirira' ameneyo? Iwe ukudziwa chimene izo zikutanthauza." Ndipo ine ndinamupereka iye kwa Billy, ndipo ndinathamangira pachitseko. Chotero ine—ine sindikudziwa momwe iwo ati adzatulukire kumbuyo uko, koma izo ziri... Ine ndimakonda kwenikweni kupita kumusi mu Louisiana, ngakhale, kwa anthu amenewo, abwino akale Akummwera kumusi uko. Koma ndiye ine ndikuyenera kudzakhala masiku omwewo ku—ku Florida, pa msonkhano wamchigawo wa Amuna Amalonda, ndipo izo zimakhala ngati zovuta pamene iwe ukuyesera kuzimanga izo pamodzi mu mphindi monga choncho.

<sup>2</sup> Ndife tonse okondwa kukhala pano mmawa uno, ndi kukhala amoyo ndi—ndi pakati pa iwo amene anganene "Ameni." Uko nkulondola. Tsopano, ine ndikupepesa kuti tonse tadzadzana muno. Ndipo iye anati ena mwa anthu anabwera ndipo anangoyendetsa nkumapita. Koma ife tiri... Ndizo zopambana zimene ife tingathe kuchita pa—panthawi ino. Inu mukudziwa. Inu mukumvetsa, ine ndikutsimikiza. [M'bale Branham akutsokomola—Mkonzi]. Mundikhululukire ine.

Kodi inu mukukhoza kundimva bwino bwino kuchokera mu *iyi* kapena kuchokera mu *iyi*? *Iyi* apa? Chabwino, ingoibweretsani iyo apa kuti ndiyiyandikire. [M'bale Neville akuti, "*Iyi* ikugwira ntchito. *Iyo* ndi—*imene*yo ndi maikrofoni yojambulira."—Mkonzi]. *Iyi*, ikujambula apa. Chabwino. Chabwino, bwana.

<sup>3</sup> Chabwino, kodi inu munasangalala usiku watha? Ine... ife ndithudi tinachipeza icho, ndipo Ambuye anatalitsa ife. Zinthu zochuluka kwambiri zimene zinganenedwe za Uthenga kumeneko, koma ine ndinaganiza mwinamwake inu mukhoza kukawerenga izo, inu mukudziwa, ndipo inu mudzazindikira, ndipo pakati pa mizere, ora limene ife tikukhalamo. Ife tiri kumapeto a nthawi kumene. Ndipo ine ndikukhulupirira zimenezo. Chifukwa, munthu aliyense wakhala akuganizira zimenezo, ine ndikuganiza, kuyambira pamene Yesu analonjeza kuti adzabweranso. Koma, inu mukudziwa, limodzi la masiku awa Iye adzabwera, mulimonse,

mwaona. Chotero ine sindikuwona kanthu katsalira kuti zichitike, kokha kukwatulidwa kwa Mpingo.

<sup>4</sup> Tsopano, basi ife tisanayandikire Uthenga umene ine ndikuwufuna mmawa uno, pa phunziro la *Kuwerenga Chotsitsa*. Ndipo tsopano ife. . . ndipo usikuuno, kumbukirani utumiki wa usikuuno tsopano, ndi *Kukhala Mu Kukhalapo Kwake*. Mukuona? Ndipo tiyesetsa kuti tifulumire, mofulumira, kuti muthe kutuluka kuti tidzapite ku ntchito Lolemba mmawa. Ndipo ndife othokoza chifukwa cha inu nonse. Ine sindikudziwa basi chimene tingati, chimene ndikanachita popanda inu. Ine basi—ine basi sindingathe kukhala opanda inu.

<sup>5</sup> Ndipo ine ndikufuna kuti ndipereke chithokoza chapadera kwa Mlongo Williams uyo, ine ndikuganiza sindikumudziwa nkomwe mkaziyo. Pamene ine ndinadzuka mmawa uno, mai, M'bale Charlie Cox anali kumeneko, ndi—ndi a—pakhomu panali patadzaza ndi zakudya, zakudya zamzitini ndi zinthu. Momwe mkazi wamng'ono wosauka uja ayenera kuti anatuluka nazo thukuta mchirimwechi, kuyika mzitini zinthu zimenezo, tomato ndi zinthu zakudya. Tsopano, zimenezo zikutanthauza mochuluka kwambiri kwa ine. Ndipo Mlongo Williams, ine ndikukhulupira iwo anasiya Baibulo lanu pamene kuti lipemphereredwe, ananena kuti ndipemphere kuti Mulungu a. . . Ine ndinapemphera mmawa uno mchipinda pamene ine ndimawerenga Uthenga, kuti Mulungu atenge zomwe ziri mu Baibulo limenelo ndi kudzaziyika izo mu mtima mwanu. Ndipo ine ndikupemphera kuti Mulungu akudalitseni inu. Ndikanakonda ndikanakulipirani inu chifukwa cha zimenezo, mlongo, ine ndikudziwa inu ndithudi munadutsa mu zambiri kuti mutuluke thukuta. Ndipo ine ndikukuthokozani kwambiri! Ndi zazing'ono kwambiri kuti ndizinene, koma ndiloleni ine ndikupatseni inu Lemba pamene ife tikudziwa, monga ine ndinanena usiku watha, sizilephera. Yesu anati, “Mochuluka momwe inu mwachitira kwa ochepa. . .” amenewo angakhale ine, mwaona, “. . . ochepa aang'ono awa a Ine, inu mwachitira izo kwa Ine.” Ndipo mulole izo zibwerere kwa inu momwe izo zikanakhallira ngati inu mukanazipereka izo mmanja Ake omwe. Mulungu akudalitseni inu chifukwa cha zimenezo.

<sup>6</sup> Zikomo inu nonse. Pamene inu muli pano, ndimapeza pa—zakhumi ndi zinthu zimene mumapereka, chimenecho ndi chidaliro chanu mwa ife, kuti izo zipite ku Ufumu wa Mulungu. Tsopano, tiri nawo udindo pa zimenezo, mwaona, ndipo tikuyenera kukayankhira pa zimenezo. Chotero ife tikufuna kuti tiyang'ane chirichonse chimene ife timachita, kuti tipange kusuntha kulikonse mwangwiro basi momwe ife tingathere, momwe Ambuye wathu angafunire izo, chifukwa sitikudziwa nthawi imene Iye adzayitanire kwa ife kuti tikayankhe ndiyeno nkudzakayankhira pa chirichonse chimene chinabwera pa njira yathu.

7 Ndi chifukwa chake ine ndikuganiza Paulo, usiku wathawu, anali ndi chikhotho chimodzi chokha. Mukuona? Iye akanakhoza kukhala nazo zochuluka, koma iye analibe. Ndicho chikhotho chimodzi chokha chimene iye akanagwiritsa ntchito nthawi imeneyo, chotero iye ankangokhala ndi chimenecho. Ine sindikuganiza kuti iye ankasamala za chuma cha mdziko. Ine sindikuganiza kuti ankasamala za kutchuka, inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza, aliyense mu kusuntha kwawo kwakukulu kwa chipembedzo monga zikukhalira lero. Ndipo anthu ambiri. . .

8 Ine ndikudziwa kuti izi zikujambulidwa. Ndipo pamene ine ndinena zinthu pano, ine ndimazindikira kuti sindikungoyankhula ndi osonkhana awa okha, koma kudutsa dziko lonse. Ndipo ine. . . Chifukwa matepi awa amapita ku mafuko ambiri, mbiri, ndipo iwo amawatengera iwo ngakhale uko mmafuko mu Afrika, kumbuyo uko, ndipo amakakhala pamenepo, ndipo mtumikiyo amawatenga iwo ndi kumawathanthauzira matepi amenewo kwa anthu, uko kumene iwo samadziwa nkomwe limene liri dzanja lamanja ndi lamanzere. Mukuona? Komwe ku Australia ndi kudutsa kumeneko kumene anthu ali—ali, samatha nkomwe. . . Chinthu chokhacho chimene iwo amadya ndi. . . Momwe iwo amapezera shuga ndi kutenga chigoba chaching'ono ndi kukakumba mulu wa nyerere ndi kumaluma pa nsana pa izo monga choncho. Umo ndi momwe amakhalira moyo pakudya shuga wawo. Ndipo iwo alibe zovala, iwo alibe kalikonse. Iwo amamutenga kangaru wokalamba ndi kumuponyera iye mmwamba pa moto, zamkati mwa iye, matumbo ndi chirichonse, ndi kumuwocha iye pang'ono ndipo kenako nkumudya iye. Ndipo ndi zimenezo, ndi zowopsya. Ndipo kumbukirani, matepi awa amakaseweredwanso kumeneko. Uthenga umene inu mukumvetsera pano umakaseweredwanso kumeneko, ndi mazana a amishonare amatenga matepi amenewa ndi kumakawasereranso iwo kumeneko, ndi kumawathanthauzira Iwo kwa anthu. Chotero, inu mwaona, pamene ine ndidzafike kumeneko pa Tsiku la Chiweruzo, inu mukuona chimene chiti chidzakhale pa mapewa anga? Nanga bwanji ngati ndinamusocheretsa winawake? Mukuona? Ndi zimenezotu. Tangoganizani za umodzi wa miyoyo imeneyo, ngati ine ndikanawasocheretsa iwo ku chinthu cholakwika.

9 Chotero ine ndiri nawo pano abale anga mmabungwe awa. Ndipo ambiri a iwo ndi amuna abwino, ambiri a iwo, ndine wokondwa ndi zimenezo. Koma ena a iwo amakhala kwambiri. . . ndipo kawirikawiri atsogoleri amafika pamalo amene amayenera kuzimangirira ndi kupanga izo ngati, oh, ngati nkhani ya ndale. Iwo amasewera ndale mmenemo. Ndipo, mmenemo, iwo amachokapo pa Mawu a Mulungu.

10 Ndipo ine ndikuyenera kukhalabe pa Mawu. Ine—ine

ndikuyenera kukhala pamenepo. Ndipo izo zikuyenera kubwera ku izi. Ndipo ine—ine—ine ndikuyenera kusuntha ndi izo, ndizo zonse. Chotero, ndipo ndife. . . Inu mukudziwa, tinkakonda kuyimba nyimbo yaying'ono, “Ife tikuyandama mu mtsinje wa nthawi, ife sitikhala nthawi yaitali.” Inu munaimvapo iyo. “Mitambo ya mkuntho ya mdima idzasanduka usana wowala.” Uko nkulondola. “Tiyeni tonse tikhale olimba mtima, pakuti sitinatsale tokha.” Uko nkulondola. “Bwato la moyo posachedwapa likubwera kudzasonkhanitsira Ngale Kwawo.” Imeneyo ndi nthawi imene ndikuiyembekezera ndiye kuti ndidzakhale ndi chikhotho chimene sichidzaperepeseka, ndi imeneyo, Yamuyaya imeneyo. Ndipo ine ndikuyenera kukhala woona kwa Mulungu, osapereka tcheru kwa zinthu pano pa dziko lapansi, kufikira tidzakafike kumeneko. Ndipo kenako ife tidzatero. . . ndizo zimene zidzakhalitse.

<sup>11</sup> Chotero ine, mu sarte izi. . . kupitirira mu zaka sarte-thuu za utumiki, ine ndayesetsa kukhala woona ku Mawu. Ine sindikudziwa za chinthu chimodzi chimene ine ndimayenera kuchisintha, chifukwa ine ndimangoziwerenga izo kuchokera mu Baibulo, kungonena chimene Baibulo linanena, ndi kuzilola izo zizipita monga choncho. Ndipo ine sindimazibwezera mmbuyo kapena kuzikonzanso, chifukwa ine ndimangonena izo momwe Baibulo limanenera izo. Ndipo, ine ndikupeza kuti, ngati Mulungu wayankhula chirichonse, ndiye ife tikuyenera tizipita ndi Mawu amenewo kuti tikawapangitse Iwo kukwaniritsidwa. Ife tinaziwona izo, monga ine ndinakuuzani inu usiku wathawu, za masomphenya posachedwapa, mwaona, kuti izo. . . Ine ndimayenera kukhala kumeneko, ndi kuchenjeza kuti ndikhala kumeneko, ndi kundiwuza ine miyezi sikisi zisanachitike kuti ndikhale pamalo amenewo, ndi kukayima pamenepo ndi kunena, “Pitani kumusi uko” (katatu) “ndi iwo.” Ndipo ine ndinangoyendabe ndi amuna enawo. Ndipo masomphenyawo anadutsa chimodzimodzi, gawo la Mulungu, ndipo ine ndinasiyidwa nditaimirira. Chotero ife tikufuna kuti tizikumbukira, inu mukuyenera kukhala pa Mawu, kungokhala basi ndi Mawu. Ndipo kumene Mawu akutsogolera, inu muzipita limodzi ndi Mawu, ndipo Iwo adzakutulutsani inu bwinobwino, ine ndikutsimikiza.

<sup>12</sup> Tsopano, ine ndikudziwa inu mwakhala muno kuyambira eyiti koloko, ndipo mwinamwake ndi teni koloko pakali pano. Ndi choncho. Chotero tiyeni tipemphere tsopano kwa Ambuye wathu. Kodi pali zopempha zapadera zirizonse? Ine ndikuwona mipango yambiri ili apa. Kwezani mmwamba manja anu pa zopempha. Mulungu akudalitseni inu. Tsopano Iye. . . Ine ndamudziwa Iye motalika mokwanira kuti ndidziwe ichi, kuti Iye amawona dzanja lirilonse ndipo amadziwa mtima uliwonse, ndipo chinthu chokhacho chimene chatsalira kuti muchite ndi kungomupempha Iye. Ndipo inu mukhulupirire zimenezo,

ndipo izo zichitika. Tsopano, inu mukhulupirire pamene ife tikupemphera.

<sup>13</sup> Atate Akumwamba, ife tsopano tikuyandikira Mpandowachifumu waukulu wamphamvu wa Mulungu, monga anthu achivundi mu thupi lachibadwa, komabe maliwu athu akuyankhula mawu amene akubwera mu Mpandowachifumu waukuluwo kwinakwake mu madera ena amene Mulungu amakhalako. Chifukwa, Yesu anati, “Inu mukawapempha Atate chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho.” Ndipo Iye anatiwuzwa ife kuti tisakayikire, koma, pamene tipemphera, kuti tizikhulupirira kuti tilandira chimene tachipemphacho, ndipo icho chidzapatidwa kwa ife. Anati, “Ngakhale inu mukhoza kudzanena kwa phiri ili, ‘Suntha,’ ndipo osakaika mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti chimene mwanena chichitika, ndipo inu mukhoza kukhala ndi chimene inu mwanenacho.” Atate, ife tikudziwa kuti zimenezo ndi zoono. Ife timaziwona izo tsiku ndi tsiku, ndipo mulibe cholakwika mu Mawu Anu. Ndi chifukwa chakuti sitimakhala pa malopo, nthawizina chikhulupiriro chathu chimalephera kutisunthira ife pamwamba pamenepo, ife timakhumudwa ndi kukayikira. Koma, mmawa uno, ife tikuyesetsa kubwera, Ambuye, ndi chiyembekezo chatsopano, titagwiritsitsa ku mzere wa moyo wa Khristu ndi lonjezo Lake. Ndipo tikubwera mu Kukhalapo kwa Mulungu kudzera mu Dzina la Yesu.

<sup>14</sup> Ambuye, ine ndikutsimikiza kuti Inu mukudziwa zopempha zonse zimene zinadziwitsidwa pansu pa dzanja mmawa uno limene linakwezedwa. Langa nalonso linakwezedwa, ndipo ilo mowirikiza limakhala lokwezedwera kwa Inu, Ambuye, chifukwa ndine munthu wosowa. Ndipo ndikupemphera kuti Inu mupereke chopempha chirichonse. Muyang’ane pa iwo, Ambuye, ndipo muyankhe zopempha zawo, kuyambira kwa wamng’ono mpaka wamkulu, kuyambira kwa zopempha zazing’ono mpaka chopempha chachikulu. Ndiye, Atate, ayankheni iwo, aliyense. Ine ndikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ndiye mukumbukire zanga, Ambuye.

<sup>15</sup> Ndipo ndikupemphera ndi kukuthokozani Inu chifukwa chotipatsa mpumulo wabwino mmatupi athu, ndi chidziwitso chimene tiri nacho cha Mawu anu, ndi kumvetsa kumene tiri nako kwa Mzimu, ndipo mowirikiza kupemphera kuti Inu mutipatse ife kumvetsa kokulirapo kuti ife tisakhale opanda pake, anthu odzitukumula ndi izo, koma anthu odzichepetsa, kuti Mzimu Woyera uthe kutigwiritsa ntchito pokwaniritsa Mawu a Mulungu, ndi kutiyika ife pamalo amene tikuyenera kukhala pa ora lino. Pakuti tikuyenera kukhala pa malo oyenera kuti izo zichitike. Ndipo ife tikufuna kutero, Ambuye. Ngati ali mayi wapakhomo kuseri kwa tebulo, ngati ziri kwa a—mwamuna wa kufakitare ali ndi sipanala mdzanja lake, ndi umboni, ngati izo ziri za mtumiki pa guwa, kapena dikoni

kapena trastii, kapena za mwana ku sukulu, wachinyamata mu zokambirana mkalasi, kulikonse kumene kuli, Ambuye, mutilole ife tikakhale kumeneko pa nthawi yoyenera. Pakuti ife tikudziwa Inu munalonjeza zimenezo, ndipo izo zidzachitika chifukwa Inu munanena chomwecho, ndipo, bwanji, ndi chikhulupiro chatu chamangidwa pamenepo.

<sup>16</sup> Tsopano, Ambuye, ife tikumverera kuti ife tiribe nthawi yotalika. Nthawi ikubwera. Ife tikutha kumverera chifunga kuchokera mlengalenga, pamene icho chikusunthira mkati. Ife tikudziwa kuti chiweruzo ndi mkwiyo wa Mulungu zakonzekera kugwa. Ife tikukhoza kumverera zotsatira zake kale. Ndipo ife tikupemphera, Ambuye, kuti Inu mutithandize ife.

<sup>17</sup> Ndipo tsopano ndithandizeni ine, Ambuye, pa Uthenga waung'ono uwu mmawa uno, wa pafupifupi maminiti sarte, wotchedwa *Kuwerenga Chotsitsa*. Tithandizeni ife, Ambuye, kuti timvetse pamene ife tiri.

<sup>18</sup> Ndipo tiyeretseni ife tsopano, Ambuye, muchotse machimo athu ndi zolakwa zathu. Ndipo mulole pasakhale munthu mmodzi pano mmawa uno, wotayika, mulole aliyense akhale wokonzeka, akhale mu bwalo lalikulu ilo pamene ife tidzakomana mbali inayo. Pamene azidzayitana, mulole ndidzamve dzina ndi dzina, “alipo.” Ndicho chimene ife tikuchiyembekezera, Ambuye. Ndipo achikulire adzakhala achichepere kumeneko kwanthawizonse, atasandulika mkamphindi ka nthawi, achisavundi, adzayima mu chifanziro Chake, dzuwa ndi nyenyezi kuti adzawale moziposa, monga Daniele ananenera, “Iwo amene atembenezira ambiri ku chirungamo adzawala ngati nyenyezi kwa nthawizonse.” Koma ife timamva zimene Inu munanena kwa mneneri, “Pita njira yako, Daniele, pakuti iwe udzapumula mmalo ako, koma mtsiku limenero iwe udzaima.”

<sup>19</sup> O Mulungu, tiloleni ife tiyesedwe oyenera kupyolera m’Magazi a Yesu, palibe zotiyenera zathu zathu zimene ife tikudzinenera, koma kupyolera mu kuyenera Kwake mulole ife tikhale oyenera kudzayima pa tsiku limenero pamene ife tikuvomereza kulakwa kwathu ndi kufuna kudzayima mu chirungamo Chake, ndi mneneri wamkulu Daniele ndi onse amene adzaimirire pamene mphotho zizidzaperekedwa. Kufikira pamenepo, Ambuye, tipangeni ife tikhale zida mdzanja Lanu. Mupange makutu athu akhale zida mmawa uno zomvetsera Mawu. Muipange milomo yanga ikhale zida zoyankhulira Iwo. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, ndipo mulole kumvetisa kwathu kumvetse chifuniro cha Mulungu. Amen.

<sup>20</sup> Ndi zovuta kwambiri kuti tiyambe. Zimawoneka ngati pamakhala zochuluka zomwe iwe unganene ndipo—ndipo umafuna kuzinena, ndipo zimawoneka ngati pamakhala nthawi

yapang’ono yoti uzinene izo. Mwinamwake ndisanati ine—ine ndisanachoke. Ine ndinanena usiku watha, ife tikhoza kupeza mwayi woti—woti mwina tidzamalizitsa limodzi la Mabuku a Baibulo, mu kugwa kwa masamba uku kapena mchisanu, tisanachoke. Ndikupita, ine ndikufuna kuti ndipite kutsidya kwa nyanja, Ambuye akalola, ikadzangotha Khristimasi nthawiina.

<sup>21</sup> Tsopano ine ndikufuna kuti inu mutsegule mmawa uno ku zowerenga, ku Ahebri mutu wa 11. Ndipo tsopano mveterani mwacheru kwenikweni ku kuwerengako. Ndikufuna kuti—kuti nditsindike pa ndime ya 3.

*Tsopano chikhulupiriro ndi chikhazikitso cha zinthu zoyembekezeredwa, umboni wa zinthu zosawoneka.*

*Pakuti mwa ichi akulu anapeza umboni wabwino.*

*Kudzera mu chikhulupiriro timazindikira kuti mayiko anapangidwa ndi Mawu a Mulungu, chotero kuti zinthu zimene zimawoneka sizinapangidwe ndi zinthu zimene zimawonekera.*

<sup>22</sup> Tsopano, umenewo ndi mutu wosamvetseka kukhala maziko a mutu umene ine—ine ndikufuna kuwugwiritsa ntchito. Zinthu sizinapangidwe kuchokera ku zinthu zomwe zimawonekera. Tsopano ine ndikufuna kuti ndigwiritse ntchito phunziro ili mmawa uno, *Kuwerenga Chotsitsa*, chifukwa ine ndikufuna kuti ndipange—kufanana mwa njira ya uneneri. Usiku wathawu ine ndimafuna kuti ndiphunzitse pang’ono pa Lemba; mmawa uno Uthenga wauneneri; ndipo usikuuno Uthenga wauvangelili.

<sup>23</sup> Tsopano, zinthu zimene zinapangidwa kuchokera ku zinthu zimene siziwoneka. Tsopano, ine ndaphunzira kudutsa mu zaka zonsezi kuti zinthu zonse zimene ziri zathupi ndi zoyimira za zinthu zauzimu, chirichonse chimene chiri mu thupi. Ndipo tsopano ingokumbukirani, kuti pamene inu muwona chirichonse mu thupi, icho chimaimira chinthu chauzimu. Mukuona? Zinthu zonse zinapangidwa motsatira zinthu zimene siziwoneka. Mwaona, zachithupi ndiye zimanyezimiritsa zauzimu.

<sup>24</sup> Tsopano, pamene ine ndimawerenga masiku angapo apitawo, ndipo ine ndikukhulupirira ine ndinazitchula izo usiku wathawu, pang’ono, kuti ine ndimawerenga pamene. . . kapena ndimamvera pa wailesi, ndikubwera kuchokera ku Canada, kumene dokotala ameneyo kuno ku United States anali—anachitira ndemanga kuti “munthu anali zaka fortini milioni za kusintha.” Iwo anafukula fupa ku Italy, mu 1800, kwina kwake mma 1800, kuti fupa ili limayenera kukhala fupa la munthu amene anali. . . mwina mwa. . . Pamene iwo akuchita izo, kuti adziwe kuti ilo linali ndi zaka zingati, ndipo dokotala uyu monga mwamuna wokalamba ndipo anayika moyo wake wonse pa kuphunzira pa fupa ili. Ndipo iye akuti, “Fupa ili ndi fupa la munthu amene ali ndi usinkhu wa zaka fortini milioni.”

<sup>25</sup> Tsopano, izo ndi zamkutu bwanji! Momwe munthu wawutayira moyo wake kutali pachabe, kuyesetsa kuti awatsutse Mawu a Mulungu, ndipo iye alibe kalikonse koma basi—kofikira kosatha kuchokera mmenemo. Ndipo aliyense amadziwa kuti ngati ukwirira fupa pansi, mu zaka twente fupalo limasinthika. Mkati mwa zaka handirede fupa limenero limadzakhala kuti latha, zimangokhala zidutswa chabe za ilo, ndipo ziribe kanthu kuti inu muliika mu chikhalidwe chotani. Mukuona? Ndipo kenako mkati mwa zaka sauzande fupa limenero lidzakhala chiyani, zaka teni handirede? Oh, lidzakhala chiyani kuchulukitsa ka teni, lidzakhala chiyani wani milioni? Kenako fortini kuchulukitsa milioni. Oh, mai! Ndizo basi. . . Si chanzeru nkomwe kuganiza za chinthu choterocho. Fupa silingakhale moyo zaka fortini milioni pansi pa chikhalidwe chirichonse. Aliyense amadziwa zimenezo. Iye ayenera kuti anatenga chinachake chimene chinkawoneka ngati fupa kapena chinachake. Ndiyeno kodi iwo akanadziwa bwino bwanji kuti ilo linali la zaka fortini million? Mukuona? Kuwonjezera apo, Mulungu anamupanga munthu padziko lapansi zaka sikisi sauzande zapitazo, ndipo izo zikukhazikitsa izo.

<sup>26</sup> Winawake amakambirana zimenezo ndi ine nthawi ina yapitayo, pa umodzi wa misonkhano yanga. Ine ndinali kuyankhula za kusinthika kwa munthu, ndipo ndinati iye anali wa usinkhu wa zaka sikisi sauzande zakubadwa zokha. Ndipo munthu uyu anati, “Chabwino, M’bale Branham, ife tikhoza kutsimikizira kuti dziko ndi la usinkhu wa zaka mamillioni. Chotero chinthu chimene inu mukuchikamba, inu nonse mukulakwitsa.”

Ine ndinati, “Kodi simumakhulupirira Baibulo?”

Iye anati, “Ndimakhulupirira kuti munthu analemba Baibulo.”

<sup>27</sup> Ndipo ine ndinati, “Zoonadi dzanja la munthu linkapanga zilembozo, koma Mzimu Woyera unkakhala kuseri kwa dzanjalo. Mwaona, linapanga chilembocho, chifukwa Baibulo linanena chomwecho.”

<sup>28</sup> Ndipo iye anati, “Chabwino, pamenepo—pamenepo, inu mukuyenera kuvomereza kuti iwo analakwitsa pokamba za dziko lapansi.”

Ine ndinati, “Baibulo silimalakwitsa, silimalakwitsa nkomwe.”

<sup>29</sup> Iye anati, “Chabwino, ngati dziko,” anati, “linali, inu mukhoza kuwona mapiri momwe iwo anasunthidwira mmwamba kuchokera ku chiphala cha moto.”

Ine ndinati, “Koma inu basi. . .”



Iye anati, “Ndipo Mulungu anapanga dziko limenero mmasiku sikisi.”

<sup>30</sup> Ine ndinati, “Tsopano, Baibulo silinanene zimenezo. Inu munangoganiza kuti ilo linanena izo.” Ine ndinati, “Tiyeni tingobwerera mmbuyo tsopano kuti tithetse mkangano wanuwo. Mutu wa 1 wa Genesis, anati, ‘Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi.’ Basi! Ndi motalika bwanji momwe Iye anali akuchita izo, ine sindikudziwa. Iye sanatiuze ife. Koma, ‘Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi.’ Basi! Kenako, ‘Ndipo dziko linali...-lopanda mawonekedwe.’” Apa ndi pamene Mulungu anayamba kuligwiritsa ntchito ilo. Mukuona? Chotero iwo amangomenya ubongo wawo pachabe. Mukuona? Mukuona?

<sup>31</sup> Mulungu anapanga dziko lapansi. Iye mwina anakhala zaka handiredede trillionsi akulipanga ilo; ine sindikudziwa kuti Iye anakhala motalika bwanji, koma Iye analipanga ilo. Ndipo Iye sananene kuti Iye anakhala motalika bwanji, ndipo si ntchito yathu kuti izo zinali zotalika bwanji. Iye anangoti, “Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi.” Basi! Izo zikukhazikitsa izo. Ndizo zonse za izo. Ndi motalika bwanji Iye anakhala akuchita izo, izo sindizo... Komano chirengedwe chinayamba kuphuka tsopano mu nthawi ina, pamene Iye anayamba.

<sup>32</sup> Ndipo ine ndikukhulupirira, kuti mmenemo, kuti chirichonse pa dziko lapansi chimanyezimiritsa Kumwamba. Ine ndikukhulupirira zimenezo, chifukwa chimene inu mumawona chirichonse chikuvutikira moyo ndi chifukwa chakuti pali moyo umene iwo umanyezimiritsidwako. Ndipo ndimakhulupirira kuti pamene Mulungu anamupanga munthu, iye anayamba kunyezimiritsa zinthu zing’onozing’ono monga ngati moyo wa nyama, ndipo kenako chinthu chotsatira chimene Iye anachilenga chinali chinachake chosiyana. Ndizo ndendende basi momwe Baibulo limati Iye anachita izo. Iye anapanga poyamba mitengo ndi moyo wa zomera, ndipo Iye anampanga munthu. Ndipo kenako chinthu chotsiriza chimene chinabwerapo kuchokera pa dziko lapansi mmawonekedwe a chirengedwe chinali munthu, palibe chapamwamba chomwe chinabwerapo. Chifukwa chiyani? Icho chinali chinyezimiritsa changwiwo cha wammwambamwamba Kumwamba, chimene, Mulungu ndi Munthu. Mukuona? Mulungu ndi Munthu, chotero izo zikutsimikizira zimenezo. Ndipo pamene Mulungu anadzatsika kuti adzakhale pakati pathu, Iye anali Munthu. Mukuona? Munthu, chotero izo zikuwonetsera kuti ungwiro wa kusintha unali Mulungu, amene ali Munthu.

<sup>33</sup> Ndipo kenako inu mutenge mtengo, (inu mutenge udzu ndi zina zotero), mutenge mtengo, iwo umanyezimiritsa Mtengo wa Moyo umene uli Kumwamba. Zinthu zonsezi zikuvutikira ungwiro. Ndipo chirichonse mu chirengedwe,

monga Ahebri amanenera apa, chinapangidwa kuchokera ku zinthu zosawoneka. Mawu ena, izo ndi zauzimu. Ndipo chauzimu chikunyezimiritsa chachirengedwe. Mukuona? Tsopano, ndiye chachirengedwe chinali Chamuyaya, kapena chikuyenera kukhala chamuyaya limodzi ndi chauzimu, koma tchimo linadzapotoza chachirengedwe. Chotero, ndipo ngati izo ziri chomwecho, chimene ine ndikukhulupirira izo ziri, ndiye chirichonse chimene chikuchitika padziko lapansi ndi chifaniziro cha zinthu zauzimu zimene zikuchitika. Mukuona? Izo zikuyenera kuwonetsera chinachake, zimene munthu wakwanitsa kuzichita.

<sup>34</sup> Tsopano, ife tikupeza, monga thupi lachibadwa, apa pali thupi lachibadwa, ndipo thupilo linapangidwa kuti lizizibala lokha, zimene zinali ana. Ndipo tsopano thupi lachibadwa, mu kubadwa kwachibadwa kwa mwana, ife tikupeza kuti chinthu choyamba chimene chimatuluka ndi madzi, kenako magazi, ndipo kenako moyo. Ife tikupeza mu thupi lauzimu la Khristu, chinthu choyamba ndi madzi, ndi Magazi, ndi Moyo; kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera. Mwaona momwe izo zimanyezimiritsira, zinthu zonse zachirengedwe zimanyezimiritsa zinthu zauzimu. Kubadwa kwachibadwa.

<sup>35</sup> Titenge, mwachitsanzo, chilumikizano cha ukwati. Ife tikupeza kuti, ukwati; timapeza chitomero, ndi mgwirizano, ndipo kenako ukwati. Izo zikuyenera kukhazikitsa izo kwa nthawi zonse. Tsopano, ndi chinthu chomwe chomwecho chimene chimadzakhala ndi Khristu ndi Mpingo. Mukuona? Chitomero, Mulungu akuitana mmitima yathu; ife timadzipereka; mwambo wa chikwati, ndipo Mkwatibwi amatenga Dzina la Mkwati. Mukuona? Mukuona? Mukuona? Ndi izo pamenepo, izo zimapanga Mkwatibwi. Tsopano, nthawizonse mkwatibwi amatenga dzina la mkwati.

<sup>36</sup> Pali zinthu zambiri zimene tingayankhulepo apa. Ine ndinalamba mndandanda apa umene unganditengere maora awiri kuti ndidutsemo, pafupifupi, ndi Malemba oti ayikire kumbuyo izi, monga ngati inu mukufuna ena a iwo apa kuti ayikire kumbuyo izo. Monga Yohane Woyamba 5:7, amasonyeza kubadwa kwachibadwa ndi kwauzimu, ndi zina zotero, “madzi, Magazi, ndi Mzimu.” Ndipo atatu Kumwamba, “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” atatu awa ndi mmodzi. Pali atatu amene amagwirizana pa dziko lapansi, iwo si mmodzi, koma amagwirizana mu chimodzi, pa dziko lapansi, ndiwo “madzi, Magazi, ndi Mzimu.” Mwaona, “madzi, Magazi, ndi Mzimu,” monga kubadwa kwachibadwa kumaimira zimenezo.

<sup>37</sup> Chotero ngati munthu akhazikika pa lingaliro la “kulungamitsidwa kuti ndizo zonse zimene iwe ukuyenera kukhala nazo,” iye akulakwitsa, akulakwitsa. Iye akuyenera kuti akulakwitsa. Ndiyeno ngati mpingo umene umakhulupirira

monga ambiri a Achipentekoste, kuti Mzimu Woyera ndi iwowo, “ndizo zonse, mungolapa ndi kulandira Mzimu Woyera,” izo ndi zolakwikabe, chifukwa iwe umayenera kupeza kuyeretsedwa mmenemo kuti uyeretse mmenemo Mzimu Woyera usanalowemo. Ngati sutero, iwe uwasiya Magazi kunjja. Mukuona? Ndipo Kubadwa kwatsopano, monga anthu amayankhulira kuti ubatizo wa Mzimu Woyera ndi Kubadwa kwatsopano. Tsopano, kumeneko ndi kulakwitsa. Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi wosiyana ndi Kubadwa kwatsopano. Kubadwa kwatsopano ndi pamene wabadwa mwatsopano. Koma Mzimu Woyera ndi pamene mphamvu ibwera mu Kubadwa kumeneko kuti ukatumikire. Ndizo ndendende. Mukuona? Mzimu Woyera ndi . . . kubatizidwa kulowa mu Mzimu Woyera.

<sup>38</sup> Kubadwa kwatsopano, umakhala ndi Kubadwa kwatsopano pokhulupirira mwa Ambuye Yesu Khristu. Mukuona? Pokhala ndi chikhulupiriro ndi kumulandira Iye ngati Mpulumutsi wako, ndiko Kubadwa, mwaona, chifukwa wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo. Tsopano, ngati inu mukufuna kuyikira kumbuyo zimenezo, tengani Yohane Woyera 5:24, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha.” Mwaona, iye ali nawo Moyo chifukwa iye akukhulupirira. Ndipo gulu lomwelo linkayenera kupita ku Pentekoste kuti likabatizidwe ndi Mzimu Woyera. Ndendende.

<sup>39</sup> Mzimu Woyera ndi mphamvu yotumikira. Chotero pamene mukamba zakuti muyenera kubadwa kenanso, ndi kuziyika izo kwa Mzimu Woyera, ambiri a Amethodisti ndi ena otero amalakwitsa pamenepo. Izo sizingatero. Izo sizingagwirizane ndi Lemba apa. Mumachiyika chinthucho cha mmbali. Muyenera kuzitenga izo momwe Lemba linaziyikira izo kunjja kuno. Mukuona? Ndipo Mzimu Woyera ndi a . . . “Inu mudzalandira Kubadwa kwatsopano zitatha izi”? Chiyani? Ayi. “Inu mudzalandira mphamvu,” Machitidwe 1:8, “pambuyo pakuti Mzimu Woyera wabwera pa inu.” Mukuona? Ndipo iwo anali atakhulupirira kale ku Moyo Wamuyaya, ndi zina zotero, koma iwo ankeyenera kuti akhale ndi Mzimu Woyera kwa mphamvu. “Inu mudzakhala mboni za Ine Mzimu Woyera ukadzaza pa inu,” chifukwa Mzimu Woyera ndi mboni ya chiwukitsiro, kuwonetsera kuti mwadzakhala wamkulu mwa Khristu.

<sup>40</sup> Tsopano, chachibadwa. Zinthu zonse zauzimu, zochitika zonse ndi zina zotero, kapena zimayimira zauzimu, kapena a—chachibadwa ndi choyimira cha chauzimu.

<sup>41</sup> Tsopano, ndinapita ku Chiwonetsero Chapadziko pamene ife tinali pafupi ndi kumeneko ku Spokane, ndipo ndinaganiza zolitenga banja.

<sup>42</sup> Chifukwa ndinakhalapo pa Chiwonetsero Chapadziko

chimodzi chokha mu United States, ndipo izo ndi pamene izo zinali mu Chicago, zaka zapitazo, Hope ndi ine tinapitako. Ndipo ife sitinakwanitse kukhalako kumeneko koma pafupifupi tsiku limodzi, akuba, ndi chirichonse. Iye anali ndi pini imene msuweni wanga anamupatsa iye, ndipo ine ndikuyenda pambali pake, winawake anadzamuchotsa piniyo. Basi...izo zinali zowopsya. Ndipo chotero ine...Tinakhala tsiku limodzi ndi kumabwerera.

<sup>43</sup> Koma ku Chiwonetsero Chapadziko, ine ndinalitenga banja ndipo tinapita kumeneko. Izo sizinali zoposa Chiwonetsero chaku Louisville pomwe pano. Inu munawona Space Needle imene iwo amayikamba, sizinali zina koma kupita kuno ku Elsby Build-...kapena Brown Building kapena kwinakwake, ndi kupita mmwamba pafupifupi maulendo eyiti kapena teni pa chokwezera mmwamba ndi kubwerera pansi. Zinali zimenezo. Ndipo ine ndikuganiza kuti General Electric ndi amene anayika izo kumeneko. Koma panali chinthu chimodzi chimene chinali chopambana. Tsopano, Germany anali ndi chiwonetsero chawo, Russia ndi mafuko ena onse anali nacho, chifukwa ndi Chiwonetsero cha Padziko lonse. A German, France, ndi ziwonetsero zazing'ono zimenezo sizinali zazikulu kwambiri kuposa momwe guwa ili lingakhalire pomwe pano.

<sup>44</sup> Koma asayansi anali nazo zawo zimene anakwanitsa kuzichita ndipo chinthu chachikulu chimene iwo anali—iwo anali kuchichita, chinali kagwiritsidwe ntchito ka fodya. Ndipo ngati munthu aliyense amene amasuta ndudu ndipo analowa mmenemo, ndipo atatulukamo ndi kumakasutanso, pali chinachake cholakwika ndi maganizo a munthuyo. Pamene ine ndinawawona iwo ndi maso anga omwe akutenga ndudu ndi kudzaiyika iyo mu makina, ndi kudzakoka a—utsi wa fodya kuchokera mmenemo ndi kudzawupumira iwo mu chubu cha mankhwala, ndipo khansa yoyera inangodzazidwa ndi iyo, ndi ndudu imodziyo. Ndiyeno iye anati, “Anthu ambiri amati,” apadziko lonse awa, zimene achita zapamwamba pa izo, anati, “anthu ambiri amati, ‘Ine sindimawukokera iwo mkati.’” Ndipo wasayansiyo anatenga nduduyo iyemwini ndipo anakokera utsi wa iyo mkamwa mwake, osati kuwuwuzira iwo kudzera mmphuno zake, kapena mulimonse momwe amawupititsira iwo mmapapo awo, koma anangowuyika iyo mkamwa mwake ndipo kenako nkudzawupumira iwo mmankhwala omwewo, munalibemo iliyonse ya khansa mmenemo. Anati, “Iyo yapita kuti? Mkamwa mwangamu. Pamene ndinameza, iyo imapita mmimba, ndithudi.” Iye anati, “Tsopano...”

<sup>45</sup> Kenako ganizo linadzabwera, “Nchifukwa chiyani madokotala amanena kuti ndudu sizoyipa?”

<sup>46</sup> Iye anati, “Munthu aliyense amene angagulitse ukulu wake wakubadwa! Dokotala atapanga neno ngati limenelo akhoza kupuma ntchito, chifukwa makampani a ndudu

amenewo angamupatse iye zokwanira kuti apume ntchito.” Iye kwenikweni amagulitsa ukulu wake wakubadwa, chifukwa iye analumbira kuti sadzachita chinthu choterocho. Koma iwo amachita izo mulimonse.

<sup>47</sup> Ndipo iye anati, “Makina ake ndi awa tsopano. Ife titsimikizira izo kwa inu mwa zomwe sayansi yakwanitsa kupanga.” Ndipo iwo anali ndi Yul Brynner, inu mukudziwa, katswiri wa pakanema mmenemo. Izo, ndi pamene kachidutswa kakang’ono ka chikonga kaja... Iye anati, “Tsopano iwo amati ‘nsonga zosefera.’” Iye anati, “Munthu amene amachita zimenezze, amangowonetera chikhalidwe cha maganizo ake. Pakuti ngati ulibe utsi uliwonse, ulibe phula lililonse, ndipo phula limapanga utsi. Ndipo ngati ukusuta ndudu yokhala ndi nsonga ya sefa,” anati, “zidzatengera pafupifupi zitanu kapena zinai kuti zikwaniritse imodzi ya inayo, chifukwa zimangotengera phula lochulukirapo kuti likwaniritse.” Ngati supeza utsi, palibepo phula. Uyenera kukhala ndi phula kuti ukhale ndi utsi. Ndiye ndi zimenezo. Anati, “Sutani, ngati inu mungasute iyo, musute imene ilibe nsonga pa iyo. Umapeza... Ndudu imodzi idzakhutitsa pamene zingatengere zitanu za zinazo, chifukwa iwe ukungokoka phula locheperapo.”

<sup>48</sup> Ndi njomba yogulitsira! Ndizo zonse zimene fuko ladzaza nazo ndi njomba za malonda, ndi uve ndi china chirichonse.

<sup>49</sup> Ndipo pamenepo ndiye iye anatenga izo ndipo anawonetsa momwe kaphukusi kakang’ono kaja kanatsakamirira mu mmero kapena mmapapo. Ndipo poyamba umakhala woyera, kenako umasanduka pinki, ndipo kuchoka ku pinki umakhala wa pepo. Kachidutswa—kachidutswa ka khungu laling’ono kankawoneka kakakulu *choncho* kudzera mu galasi, koma, ndithudi, mukatenga galasi lamphamvu kuti muwonere ngakhale khungulo. Kenako iye anati, “Pamene iwo usanduka wa pepo, inu muli ndi khansa.” Iye anati, “Mwamuna amene angasute paketi imodzi ya ndudu patsiku amakhala ndi mwayi wokwanira kasevete pa handiredi wakufa ndi khansa kuposa munthu amene samasuta iyo.” Ndipo zimawoneka zopusa kutenga mwayi woterowo.

<sup>50</sup> Tsopano, ndipo kenako iye anatenga chinthu china ndipo anatsimikizira icho, iye anam’bweretsa khoswe woyera. Ndipo anatenga ndudu ndipo anadzaiyika iyo mmakina, ndipo anadzaikokera iyo kudutsa mtundu wina wa chinachake chonga nsangalabwi yoyera, ndipo anatenga a—thonje, ndipo anatenga chikonga chimene chinali mu ndudu imodzi ndipo anadzapaka pa nsana wa khoswe. Masiku seveni aliwonse iwo ankatulutsamo khoswe wina. Ndipo iwo amakhala naye aliyense pa phunziro la tsiku limenero. Ndipo ankamulowetsa khoswe ameneyo kwa masiku seveni ndi kudzamutulutsa iye, khansa amayima mokwera *choncho* pa nsana wa khosweyo. Ena a iwo sankakhala moyo ngakhale masiku seveni. Khosweyo

samatha kuyenda. Ine sindinathe kudya kwa masiku awiri kapena atatu, nditayang'ana pa chinthu chonyansacho, atayima pamenepo ndi khansa, ndipo iyo ikuyenderera mmusi pa miyendo yake ndi zinthu monga choncho, khansa yayikulu yotalika kwambiri inatupa pafupifupi theka la inchi pa nsana wa khosweyo, chifukwa cha chikonga chochokera mu ndudu imodzi. Ndipo inu mukuganiza kuti zimenezo zinawaletsa iwo? Bambo wamkulu atakhala pafupi ndi ine pamenepo, ndipo thukuta likuyenderera pa nkhope yake, anati, “Zikukhala ngati zokhudza, sichoncho izo?”

Ine ndinati, “Inu mumasuta?”

Iye anati, “Inde, bwana, ine ndimatero.”

<sup>51</sup> Ine ndinati, “Chabwino, ndiye inu muyenera kuti musiyе zimenezo.” Koma ndi zimenezo, zomwe akwanitsa kuzichita, zimene angatsimikizire kuti zimachita zimenezo.

<sup>52</sup> Tsopano, ine ndikuneneratu kuti dziko layima ndipo ngati chitukuko chiripo, kumbuyo mu nthawi ya chiletso pamene pankakhala chindapusa kugulitsa botolo la kachasu, izo zingakhale kuchulukitsa ka teni chindapusa chimenecho kugulitsa paketi ya ndudu mu zaka zingapo kuchokera pano, ngati chitukuko chiripo. Ndi zoyipa ka teni kuposa kachasu. Izo ndithudi ziri. Izo ndi—ndi chiphe, zimenezo. Ndipo iwe ukhoza kuwauza anthu za zimenezo, ndipo iwo samapereka chidwi chochuluka kwa izo. “Ndi mlaliki woyera wodzigudubuza,” ndi kuzisiya izo. Mwaona, ndi zimenezotu, iwo sakuzindikira.

<sup>53</sup> Koma, mfundo yanga ndi iyi, chimene zinthu za sayansi zakwanitsa kuzichita. Iwo anali kumeneko ku Chiwonetsero Chapadziko, amawonetsa mwa kafukufuku wa sayansi zimene sayansi yakwanitsa kuzichita mu zinthu zachirengedwe. Tsopano, ife tiri pano kudzawonetsa mwa kafukufuku wauzimu zimene Mulungu wakwanitsa kuzichita ndi anthu amene adzakhulupirire Mawu ake. Tsopano, kuti mukwaniritse zinthu zasayansi, mukuyenera kugwira ntchito mumizere ya sayansi. Kuti mukwaniritse zinthu zauzimu, mukuyenera kugwira ntchito mu mizere ya zauzimu. Tsopano, mukuganiza kuti khoswe ameneyo amawoneka mowopsya, momwe iye ankawonekeramo, inu mukanati mumuwone iye! Ndikanakonda ndikanakhala ndi chithunzi chake, nkomwe, kuti ndikusonyezeni. Ngati ine ndikanakhala nacho icho, ine ndikanatero, koma iwo sangakulole kuti iwe ukhale nacho icho. Koma zindikirani. Ndithudi, khosweyo amangokhala maora angapo, ena a iwo samakhala nkomwe masiku seveni. Koma taganizani za zimenezo!

<sup>54</sup> Inu mukuganiza kuti izo zinkawoneka kakata, inu mumayenera kuwona momwe moyo umawonekera umene wakana Uthenga. Inu mukuyenera kuyang'ana momwe iwo aliri chinthu chowoneka-moyipa. Momwe mdierekezi amamugwirira

munthu ndipo akhoza kumupotoza mwana wa Mulungu kukhala chinthu chowoneka moyipa, monga amawonekera mmaso a Mulungu. Oh, iye akhoza kukhala wantali mapazi sikisi, ndi mapewa ngati ine sindikudziwa chiyani, ndi tsitsi lopiringizika ndi *chiyani*, izo sizikutanthauza kanthu. Ndi chamkati mwa munthu chimene chiri chokhalitsa. Chakunjachi ndi fumbi, mulimonse.

<sup>55</sup> Chotero ndi chimene achita, ndiyeno iwo amawonetsa, anali ndi singano ya mmwamba iyi ndi chirichonse, zimene iwo ankawonetsera kuti akwanitsa kuzichita, zimene iwo anali atakwanitsa kuzichita, ndi kufotokoza ma atomiki awo onse ndi zina zotero. Iwo anali ndi kulosera kwa zomwe Chevrolet idzakhale. General Motors inali nayo pa chiwonetserocho, chimene...mwa ina, mu zaka zotsatira, chimene Chevrolet ya mu zaka za zana la makumi awiri idzawonekere. Iyo inkawoneka kwa ine ngati a—paipi ya gasi yokhala ndi chotchinga pamwamba pake. Tsopano, iwo anawonetsa momwe iyo izidzagwirira ntchito ndipo izidzayendetsedwa ndi mphamvu ya atomiki ndi mtundu wina wa phiko limene lizidzanyamulana lina ndi limzake ndi kumalamulira. Iwo udzakhala a—mwayi waukulu.

<sup>56</sup> Koma ndikudabwa ngati ife tingatsegule mmbuyo mu masamba a Bukhu la Mulungu, mmawa uno, ndi kuwona momwe mpingo uti udzawonekere pa nthawi imeneyo, kuwona zimene Mulungu wakwanitsa kuzichita. Oh, momwe zochitika nthawizonse mdziko lapansi lino zimaimira chinachake chimene chikuchokera kwinkawake; koma pamene izo zikantha dziko lapansi, izo kawirikawiri zimakhala mchikhalidwe chopozedwa chifukwa izo zimakhala mdziko la mdima ndi tchimo. Mukuona? Koma ndiye pali choyimira choona mmadera auzimu a gawo linalo. Kuchokera pokhala mmadera atatuwo, ndiye gawo la chisikisi limakhala ndi choyimira chake. Ndine wokondwa kwambiri ndi zimenezo.

<sup>57</sup> Tsopano, tiyeni tingotenga zimene takwanitsa kuzichita tsopano zimene takwanitsa kuzipanga zaka zingapo zapitazi. Tsopano, tiyeni tiyambe pa chinachake chimene chinachitika. Ine sindikusungani inu motalika, Ambuye akalola, koma ine ndikufuna inu muwone ichi mwamsanga. Ndipo, oh, pamene izo zinafika kwa ine, ine ndinamverera ngati ndiwulukire kutali. Tsopano zindikirani, tsopano, zaka zingapo zapitazo maulendo anali pa akavalo ndi ngolo, osati kale kwambiri, kale kale. Ine ndinkayenda mozungulira pa kavalo ndi ngolo, ndi pa chishalo. Pamene ine ndinali mnyamata, usinkhu wa zaka fiftini, sikisitini, ine ndinkakwera kavalo, ndipo ndinkapita ku tauni pa kavalo ndi ngolo, ndinkayendetsa pafupi ndi tchalitchi ichi kuno, msewu wamatope kunja uko, ndi dambo kuno lodzaza ndi udzu wautali ngati nyumbayi, pafupifupi, ndi kavalo ndi ngolo, ndikuperekerera nyemba ndi zinthu zochokera ku munda.

58 Lero ndimazidutsa izo mu galimoto. Ndi kusiyana kotani! Tsiku la kavalo ndi ngolo, kenako tsiku la galimoto.

59 Ndipo kenako tsiku la ndege linadzabwera motsatira, imene inkanyamuka kuchoka pa dziko nkupita mu mlengalenga. Tsopano, ngati inu mungawone, motsimikiza basi monga zokwanitsa kuchita zimenezo zinali mwa sayansi, ngati munthuyo adzakhale ndi malingaliro auzimu ndi kumvetisa, izo zimaimira zokwanitsa kuchita za chuma cha Mulungu ndi Mpingo Wake. Tsopano masiku. . .

60 Ndipo, kumbukirani, mtumiki nthawizonse amabwera kumapeto a Uthenga. Ife tikudziwa mu mibadwo ya mpingo umo momwe ife tinazipezera zimenezo.

61 Tsopano, masiku a kavalo ndi ngolo anali ndani? Kumeneko kunali kutha kwa m'badwo wa Chilutera. Mwaona, masiku a kavalo ndi ngolo. Iwo ankakhulupirira mu kulungamitsidwa. Mulungu akuwubweretsa Mpingo kuchokera ku Chiroma, Chikatolika, Iye anawubweretsa iwo mu zokwanitsa kuchita zoyamba zauzimu, kuti, "Olungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro." Amenewo anali masiku a akavalo ndi ngolo, pamene iwo ankachokera ku. . .ku masiku a kavalo ndi ngolo, amenewo anatha.

62 Tsopano, chokwanitsa kuchita chimene munthu anali nacho pa njira ya mayendedwe chinali galimoto. Ndipo, inu mukuzindikira, galimoto imeneyo imawonjezereka nthawi zonse, mu mphamvu zake.

63 Tsopano, pa mapeto a m'badwo wa Wesley, unabweretsa pokwanitsa kuchita mwauzimu, kuyeretsedwa, zimene zikutanthauza kuti mpingo unakwezedwa kuchokera ku chikhalidwe cha kulungamitsidwa unapita ku chikhalidwe cha kuyeretsedwa.

64 Tsopano, ine ndikufuna inu kuti mukumbukire izi pamene ife tikupitirira, kuti mpingo umene umatchedwa "mpingo" si Mpingo. Mpingo ndi Mpingo, wauzimu! Makumi a masauzande kuchulukitsa masauzande a Achilutera amene anajowina mpingo, sankadziwa nkomwe za kulungamitsidwa kuposa momwe nkhumba inkadziwira za chishalo chammbali. Iwo—iwo sankadziwa kanthu za izo. Ndipo mu m'badwo wa Wesley, momwe makumi a masauzande ankadzinenera kuyeretsedwa, iwo sankadziwanso za mphamvu yoyeretsa ya Mulungu kuposa—kuposa momwe kalulu amachitira ndi nsapato za chipale. Mwaona, iwo mwamtheradi sankadziwa izo.

65 Koma panali anthu amene anakwanitsa kuzichita zimenezo. Aleluya! Inu mukuona kumene ine ndikupitako. Panali winawake amene ankadziwa chimene "kulungamitsidwa" kumatanthauza pamaso pa Mulungu, "kukhala ndi mtendere ndi Mulungu kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu." Panali ena a Achilutera amenewo amene anali okhulupirika.



Iwo ankakhulupirira Iwo. Zinalibe kanthu chimene mpingo wa Katolika unkanena, iwo ankakhulupirira Mawu a Mulungu ndipo anayima pa Iwo chifukwa mtumiki wa m'badwo umenewo analalikira “olungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro,” ndipo iwo ankakhulupirira mu chikhulidwe cha kulungamitsidwa. Ndipo iwo anali okhoza mwa chisomo cha Mulungu kukwaniritsa kulungamitsidwa, kukhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

<sup>66</sup> Tsopano, ife tikuzindikira kachiwiri, motsatira panadzabwera Amethodisti ndi kuyeretsedwa. Analipo ochuluka a Amethodisti amenewo amene anali oyeretsedwa kwenikweni. Tsopano, alipo ambiri a iwo akudzinenera izo ndipo samadziwa kanthu za zimenezo. Mpingo wa Methodisti unkaphunzitsa kuyeretsedwa. Iwo ankati iwo ankapita kumeneko ndi kumakalira ndi kumabwererako, anati, “Ulemelero kwa Mulungu, ine ndayeretsedwa!” Ndipo ankapitirirabe kumakakhala moyo monga iwo nthawizonse ankachitira. Koma ena a amuna amenewo ndi akazi anali oyeretsedwa kwenikweni ku zinthu za mdziko, ndipo ankakhala moyo wodzipatula, moyo wapadera. Chifukwa chiyani? Uwo unali m'badwo wa magalimoto umene unkatenga mphamvu zambiri za akavalo. Galimoto, T-model yakale mwinamwake inali ndi mphamvu za akavalo fifitini kapena twente. Mwaona, inali ndi akavalo fifitini kapena twente atayikidwa mu injini yaing'ono monga choncho. Kuyeretsedwa! Pamene sayansi inakwaniritsa chinachake mwa—mwa—mwa chithupi, Mulungu akukwaniritsa chinachake mwauzimu. Mwaona, chinachake chikuchitika nthawi zonse. Ndipo kenako utatha m'badwo woyeretsedwa...

<sup>67</sup> Tsopano, timutenge munthu ngati Bevington wokalamba. Munthu, ndani akanakhala munthu wamkulu kuposa M'bale Bevington wokalambayo? Ndipo tayang'anani pa John Wesley, George Whitefield, Finney, Knox, ambiri a Amethodisti akale amenewo amene anakhetsera thukuta. Iwo anadutsa mu gehena pa dziko lapansi, kuzunzika, chifukwa iwo ankakhulupirira kuti Mawu a Mulungu amaphunzitsa kuyeretsedwa, sitepe yachiwiri ya chisomo, ndipo iwo anakhala ndi icho, ndipo iwo anachikhulupirira icho, ndipo iwo anachita zodabwitsa ndi icho. Chimodzimidzi basi monga Henry Ford ndi iwo anachitira ndi mayendedwe a Ford yakale ya model-T pambali pa kavalo, iye anapitirira ndipo pamwamba pa tsiku la kavalo. Ndipo Wesley anapitirirabe mpaka pamwamba pa tsiku la Chilutera.

<sup>68</sup> Ndipo kenako motsatira panadzabwera Pentekoste. Ndipo monga sayansi ya mdziko inatha kukwanitsa—injini ya galimoto, a Wright Brothers amene analenga kapena kupanga, kukonza, kani, ndege, makina owuluka anali patali pamwamba pa galimoto padziko lapansi, chifukwa iye anaitengera mu mlengalenga. Tsopano, a Wright Brothers, kupyolera mu

zimene anakwanitsa kuzichita, anakhoza kuitenga sayansi ndi kudzafanizitsa chinachake kuno pa dziko lapansi, kuti akawonetsere kuti kunali chinthu chachikulu chauzimu chimakonzekera kuti chidzachitike. Ndipo pamene a Wright Brothers anakwanitsa kuwachotsa mapazi a munthu pansi, Pentekoste inadzagwa ndipo anadzatengera mu mlengalenga ndi mphatso yauzimu, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Iye anatengera mu mlengalenga! Oh, aleluya! Anachotsa mapazi ake pansi kuti akhoze—iye azikhoza kusambira pozungulira, anakwera mmwamba mu mlengalenga! Oh, momwe iye anapitira pamwamba pa akavalo ndi ngolo! Momwe iye anapitira pamwamba pa galimoto! Iye anali mmwamba mu mlengalenga. Iye anali akugogoda ndi kumapuma ndi kumagunda, koma iye anali akuwuluka. Mwaona, chimene munthu akukwanitsa padziko lapansi, pakuti izo zimapangidwa ndi zinthu zimene sizimawoneka. Mulungu anali wokhoza kukwanitsa chinachake mwa anthu odzazidwa ndi Mzimu amene anali ndi njala ndi ludzu, ndi iwo amene akanati adzakhale ndi Mawu.

<sup>69</sup> Tsopano, ngati Wesley akanapanda kuchoka pa Mawu ndi kukhala ndi dzina loyipa kumbuyo kwake, ankatchedwa munthu wopenga, ndi china chirichonse, iye sakanakhoza konse kukwanitsa. Koma Wesley anali mmodzi wa asayansi aakulu a Mulungu. Luther anali mmodzi wa asayansi aakulu a Mulungu. Iwo sankasamala chimene mipingo inkanena, chimene mabungwe ankanena. Luther sankasamala chimene Akatolika ankanena, iye ankakhulupirira kuti olungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro! Aleluya! Ndipo iye anatenga mankhwala a Mulungu a Mawu ndipo anawayika iwo pamodzi, ndipo mpingo unkasuntha mwa chikhulupiriro. Wesley anadzaziyika izo pamodzi mwa Magazi, ndipo anadzazitsimikizira izo mwa Magazi, ndipo mpingo unayeretsedwa. Achipentekoste ankakhulupirira ubatizo wa Mzimu Woyera, kuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo akutali, ndipo iwo anayika mankhwala pamodzi kuchokera mu Mawu, ndipo iwo anasunthira mlengalenga. Aleluya! Iwo anatuluka, chifukwa iwo anali okhoza kuti athe kukwaniritsa zimenezo.

<sup>70</sup> Tsopano, nchifukwa chiyani amuna awa anachita izi? Nchifukwa chiyani Luther anapeza izo? Nchifukwa chiyani Wesley anapeza izo? Nchifukwa chiyani ena onsewa? Chifukwa zipangizo zinali pansi pano zimene zikanakhoza kupanga Ford ya T-model. Panali magetsi amene akanatha kupangitsa a—galimoto kuti iziyenda. Panali mafuta pa dziko lapansi, panali mapistoni ndi zina zotero, zimango zonse, mpweya wa jenereta, ndi chirichonse chimene iwo anali nacho kuti alenge chinthu ichi, ndipo zindikirani icho chinayamba . . . kupanga icho, kani, osati kuchilenga icho. Mulungu ndiye Mlengi, Iye anali nazo ziri apa. Koma munthu amene ankakhulupirira izo mu gawo

la sayansi, la chirengedwe, anafufuza mu izo, ndipo iwo samatenga “ayi” ngati yankho. Iwo amakhulupirira izo. Ilo linali vumbulutso mu mtima mwawo, ndipo iwo ankakhala nalo ilo mpaka iwo ankatsimikizira kuti ilo linali lolondola.

<sup>71</sup> Umo ndi momwe John Wesley anatsimikizira kuyeretsewa. A—zipangizo zinali apa, Mawu a Mulungu amene anabweretsa izo. Iye anakhulupirira izo! Zinalibe kanthu ngati mpingo wonse, mpingo wa Anglican ndi onse akanamukana iye, iye anakhala ndi kukhudzika kwake ndipo iye anatsimikizira izo. Ndipo Achipentekoste anadzabwera ndipo anadzatsimikizira, chifukwa iwo anali ndi chogwirika, kuti Mzimu Woyera unali wolondola. Ndipo iwo anakwera mpaka mu mlengalenga.

<sup>72</sup> Kodi inu munazindikira, chimodzi—chimodzi cha zimene sayansi inakwanitsa kuzichita ndi chinacho, chinathandizira chimzakecho. Iwo anali mawonekedwe chabe apamwamba. Mukuona? Galimoto inali mayendedwe okwera kwambiri kuposa kavalo, ndipo ndege inali mayendedwe apamwamba kuposa galimoto, koma izo zinatsatana china ndi chimzake. Mphamvu za kavalo! Ameni! Ngati imeneyo ndi mphamvu ya kavalo, nanga bwanji mphamvu ya Mulungu? Nanga bwanji Mzimu Woyera ndi mphamvu? Mphamvu ya Mzimu Woyera imene ikhoza kukulungamitsani inu, mphamvu ya Mzimu Woyera yomweyo ingakhoze kukuyeretsani inu. Mphamvu ya Mzimu Woyera yomweyo imene imakuyeretsani inu, ikhoza kukudzazani inu ndi Kukhalapo Kwake. Ndipo sayansi pang’ono, amene sankadziwa ma ABC awo, inazipeza izo. Chifukwa? Iwo anali asayansi auzimu. Ameni. Iwo anachiwona chinthucho, iwo anachikhulupirira icho. Munthu anazichita izo mwa maphunziro, wasayansi wachirengedwe. Wasayansi wauzimu anachita izo mwa vumbulutso. Mmodzi mwa maphunziro, wina mwa vumbulutso. Oh, ngati ife tingathe kungotseguka. Pali mitundu yonse ya zinthu zimene ziri apa. Uko nkulondola.

<sup>73</sup> Tsopano ife tikuzindikira momwe izo zimayendera, momwe Mulungu anakwaniritsira izo. Mwa Achipentekoste, anazitengera mu mlengalenga. Momwe iwo... Kenako anabwezeretsedwa ku mpingo, machiritso, kuyankhula mu malirime, vumbulutso, mphatso za Mzimu. Mwakuti, Luther sanadziwe kanthu za izo, ngakhalenso Wesley. Iwo sankaphunzitsa konse zimenezo, iwo sankadziwa kanthu za izo. Izo zinali kunja kwa m’badwo wawo.

<sup>74</sup> Bwanji, kodi Henry Ford akanadziwa chiyani za ndege mu tsiku limenero a Wright Brothers asanabwere? Mwaona, iwo sakanazidziwa izo. Kenako chinthu chomwecho chimene a—munthu kumbuyo uko ndipo akuyendetsa kavalo ndi ngolo, zaka faivi handirede zapitazo, sakanadziwa kanthu za ngolo yopanda kavalo, Baibulo lokha linati iyo idzakhala pamenepo. Chotero iwo anatha kukwaniritsa izo mwa kufufuza kwa sayansi.

Ndipo pamene izo zinadzachitika pa dziko lapansi, Mulungu anaziimira izo mwa chokwaniritsa cha Mpingo Wake. “Pakuti zinthu zimene ziripo, zowoneka, zinapangidwa kuchokera kwa zinthu zosawoneka.” Mwaona, chinyezimiritsa cha izo.

<sup>75</sup> Tsopano, tsopano m’badwo wa Pentekoste, kwa zaka fifite zapitazi, watumiza chitsitsimutso kuzungulira dziko, ndi mitundu yonse ya chirichonse mmenemo. Ndipo amakhala nawo machiritso, ndipo matenda amachiritsidwa, olumala amachiritsidwa, akhungu amabwezeretsedwa kupenya kwawo. Kodi inu mukuganiza kuti dziko linkakhulupirira zimenezo? Ayi, bwana. Iwo sanamukhulupirire Luther. Iwo sanamukhulupirire Wesley. Iwo sanawakhulupirire Apentekoste. Koma Mulungu anatenga Baibulo, mu kafukufuku wake, mwamuna amene anali wololera kuti achite zimenezo, anatenga Baibulo ndipo anatsimikizira kwa ilo kuti Ilo linali lolondola. Ameni. Tsopano ife tikuyenera kukumbukira zimenezo, ife tikuyenera kuzikhulupirira izo, powona kuti zinthu zimenezo zinali choyimira. Tsopano tawumalizitsa m’badwo wa Chipentekoste. M’badwo wa Chipentekoste, monga ine ndatsimikizira kumeneko, ukudzalowa mu m’badwo wa Laodikaya.

<sup>76</sup> Koma tsopano chinachake chachitika. Ife tiri ndi wa muchombo tsopano. John Glenn anali wa muchombo wathu woyamba. Ndipo ife tikupeza kuti izo ziri patali kwambiri pamwamba pa ndege, ndege imangotha kupita monga mwa mphamvu yake ndi zina zotero. Koma iyi ndi mphamvu ya atomiki, mphamvu yayikulu imene imamupititsa iye mokwera kwambiri kuposa ndege, ngakhale ndege—si imeneyo nkomwe. Uko nkulondola. Iye wakwanitsa kuchita zimenezo. Chabwino. Tsopano ife tiri ndi wa muchombo, m’badwo wachirengedwe.

<sup>77</sup> Ndipo, kumbukirani, wa mthenga amabwera ku mapeto a uthenga woyamba, nthawizonse. Ife tazitsimikizira izo pamenepo. Tsopano tiri pa mzere wa wa muchombo. Ameni ndi ameni! Mulungu wa . . .

<sup>78</sup> Sayansi yakwanitsa kutsimikizira kuti alipo wa muchombo amene akhoza kupita patali kwambiri mpaka inu simungathe kuchiwona icho ndi maso anu achibadwa, ndipo icho chikhoza kupita kaya kuli mphamvu yobweza iliyonse kumeneko kapena ayi. Iye akhoza kumangopitirira chifukwa ali mu thanki yampweya, ndipo iye akhoza kupita kumeneko ndi kumakayendako ndi kumakawona mayiko kozungulira. Wa muchombo! Oh, mai, ndi m’badwo wanji umene ukubwera. Inde, bwana, kupita kudutsa zinthu zachirengedwe zirizonse nkomwe, ndi kusesa mpaka kutsidyako.

<sup>79</sup> Kodi izo zikuimira chiyani? M’badwo wauzimu, nthawi yauzimu kumene Mulungu ati adzakhale ndi a muchombo auzimu. Ameni! Iwo ali pano pompano! Aleluya! Mphungu

za mu mlengalenga zimene zikhoza kupita mmwamba kuposa mbalame iliyonse, zimauluka pamwamba pa chirichonse, amuchombo auzimu (Ulemelero!) amene akhoza kuwatenga Mawu a Mulungu ndi kutsimikizira kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Wa muchombo wauzimu! Oh, mai! Ulemelero! Izo zimandipangitsa ine kumverera bwino, kukhala mu m'badwo uno! Tsopano ndi chinthu chodabwitsa bwanji kwa wa muchombo wauzimu! Mukuona? Icho ndi chiyani? Kodi asayansi achibadwa anachita chiyani? Atha kukwaniritsa zimenezo. Ndipo Mulungu, kudzera mwa munthu amene amakhala ndi Baibulo ndi kunena kuti "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse," ndipo osawopa lonjezo mosasamala za chimene aliyense anena, kukhala nalo ilo. Icho ndi chiyani? Iwe umakhala wa muchombo amene akhoza kupita patali kwambiri kupitirira kuganiza kwa chipembedzo. Icho ndi choposa china chirichonse. Icho chaposa zinthu za mpingo. Kunja uko kumakhala ndi Mulungu ndipo Iye yekha. Amuchombo!

<sup>80</sup> Ndipo, kumbukirani, kuti iwo akhale a muchombo, iwo ankayenera kuti alowe mu thanki, ndipo iwo samatha kudzilamulira okha. Zimatengera mphamvu ya mu mlengalenga, mphamvu ya atomiki kuti imukweze iye kupitirira mlengalenga, ndipo zikatero iye amalambuliridwa ndi nsanjayo. Ulemelero! Amuchombo a Mulungu ndi chimodzimodzi! Iwo amabwera mu thanki, ndipo amadzalowa mmalo, amadzalowa mthupi, ndipo thupi limenero ndi Thupi la Khristu. Ndiye, si iwowo, si—si choncho, sanali John Glenn, anali—inali thanki imene iye analimo. Iwo anali makina. Iye ankangokhala mmenemo, iye sankachita kanthu kalikonse. Iye ankangokhala ndi kulimba mtima kwenikweni kuti akwere mmenemo ndikuti "ndi zoonadi," chifukwa sayansi inali itatsimikizira izo.

<sup>81</sup> Mulungu akufuna munthu amene angathe kubwera mwa Khristu ndi kukhulupirira kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndipo osatenga kuganiza kwawo kwawo, kusunthira kunja mu mlengalenga, olambuliridwa ndi Mzimu Woyera. Amen. Amuchombo! Psyii! Izo ziri patali bwanji ndi kavalo wakale ndi ngolo! Izo ziri patali bwanji ngakhale ndi ndege! Izo ziri patali bwanji ndi kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera! Iwo akubwera ku mphungu. Poyamba, iwo anali abuluzi, kenako anasanduka nkuku, kenako iwo anadzakhala akhwangwala, koma tsopano iwo ndi mphungu. Palibe amene angawatsatire iwo!

<sup>82</sup> Mphungu ndi mbalame yapadera. Iyo ikhoza kupita mmwamba kuposa mbalame ina iliyonse. Iyo imakhala yokonzeka kuti iziwona, imakhala ili ndi mutu watcheru ikakafika pamwambapo. Pali anthu ena amene amatha kudumpha mmwamba ndipo osadziwa kumene iwo ali akafika kumeneko, chifukwa iye sangawone kutali kuposa mmene iye

walumphira. Koma pali ena amene akhoza kuyang'ana mmbuyo ndikuwona zimene zikuchitika. Imeneyo ndi mphungu. Iye akhoza kuyima pamenepo mpaka nkumaziyang'ananso izo, ndi kumadikirira mpaka atamva uthenga umene ungamuuze iye choti anene. Ameneyo ndi wa muchombo wa Mulungu. Mukuona? Izo zatsatira zina zonse zimene zinakwanitsidwa kuchitidwa, bwanji izo sizikutsatira chochitidwa ichi?

<sup>83</sup> Amuchombo a Yesu. Amen. Samanyamuka nkomwe ndi mphamvu yake yomwe. Iye amachitidwa kupatsidwa mphamvu. Chinthu chokhacho chimene iye amachita ndi kulowa mmenemo. Ndizo zonse zimene inu mukuyenera kuchita, ndi kulowa mmenemo, Mulungu adzachita kutumizako ndi kukhazikitsa. Iyo si mphamvu ya mafuta aponso, komanso, kachikhulupiro kena ka mpingo. Ndi mphamvu ya atomu ya Mulungu imene imakukankhirani inu kuchoka mlengalenga kupita mu danga uko. Amen. Oh! Bwanji, icho ndi chiyani, amuchombo awa? Iwo ali ndi... Iwo samasowa konse... anangotenga mawu oti kulungamitsidwa, mawu oti kuyeretsedwa, iye amakalowa mu Baibulo lonselo. Amen. Iye amakalowa mu zonsezo, chifukwa iye amadziza kuti Mulungu ndi wokhoza kuchita lonjezo lirilonse limene Iye anayamba walipangapo. Iye amangokhala pamenepo ndi kumadikirira. Oh, mai! Mawu amakhala okakamizika kuti adziwonetsere Okha. Ngati inu mukudwala, ndipo wa muchombo, mungokumbukira, lowani mwa Khristu, dikirani kuwerenga chotsitsa. Ndizo zonse. Iye adzawombera chipolopolocho, musadandaule. Tsopano, akhoza kukwaniritsa zimenezozo chifukwa Mulungu analonjeza izo.

<sup>84</sup> Tsopano, wa muchombo ndi wamkulu bwanji, zinthu izi tsopano, kuchokera ku mphamvu yakale ya kavalo, mphamvu ya galimoto, ndi—ndi mphamvu ya ndege! Inu mwaona, wa muchombo, iye amakhala mmwamba kwambiri mwakuti iye amakhoza kuwona zinthu zimene munthu wa pa kavalo ndi ngolo sangathe kuziwona. Iye amakhala pamwamba kwambiri moti akhoza kuwona zinthu zimene munthu mu galimoto sangathe kuziwona. Iye amakhala pamwamba kwambiri moti akhoza kuwona zinthu zimene munthu woyendetsa ndege sangathe kuziwona. Iye wapita kutali kunja kwa kulingalira. Amen. Ulemelero! Ndi zimenezotu. Iye wapita kudutsa zokhoza kuzikwaniritsa zirizonse zimene munthu angakhoze kuziganizira, bungwe, chipembedzo, “Iwe uyenera kukhala wa Methodist, Baptisti, kapena kukhala wa *uwu*, a umodzi, uwiri,” kapena chirichonse chimene icho chiri. Iye ndi wa muchombo, iye wapita mpaka mu mlengalenga. Amen. Ndine woyamikira bwanji!

<sup>85</sup> Ndipo, kumbukirani, wa muchombo amalamulidwa ndi mphamvu ya mlengalenga. Inu munawawona iwo akumubweretsa John Glenn mmenemo. Ine ndinayang'ana

kumusi uko ku Cape Canaveral ndipo ndinawona chinthu cha mmlengalenga chachikulu chija, ndipo iwe sukanamuwona iye nkomwe paliponse, koma iwe umatha kudziwa kumene iye anali mwa njira imene choyendetserachi chimalozera. Uko ndi kumene iye anali. Mukuona? Ndipo ife tiri ndi choyendetsera, nafenso, pemphero. Pemphero ndi mphanvu yoyendetsera imene imatsogolera wa muchombo. “Apempheni Atate chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho.” Mukuona? Mungoona momwe pemphero likuyendera, inu mukhoza kuwona momwe iye akulozera. Amen. Mungowona momwe mpingo ukupempherera, mukhoza kuwona momwe mizinga idzawulukire. Mukhoza kudziwa izo ndi—ndi momwe amu chombo akuyendera, momwe mpingo ukupempherera.

<sup>86</sup> Iye amapemphera, “Ambuye, ndithudi ife sitimakhulupirira mu zinthu izi.” Uh-oh! Wa muchombo uja akutsika pansi. Ndizo zonse. Oh, m’bale!

<sup>87</sup> Koma pamene zinthu zonse ziri zotheka, “Ambuye, tsanulirani Mzimu Wanu pa mpingo ndipo muwupatse iwo chimene ife tikuchisowa. Mutsanulire pa ife Mzimu Woyera, ndipo mungotichotsa ife mu kulingalira kulikonse, ndi kukhulupirira kuti Mawu amenewo ndi owona ndipo ife tidzayima ndi Iwo.” Kuwona chopimba ndiye nkuyamba kukweza mutu wake monga chonchi, mwaona. Wa muchombo akupitirira ndi kupitirira ndi kupitirira, mmwamba mu mlengalenga. Hum! Zodabwitsa! Amapita kudutsa chipembedzo chirichonse, amapita kudutsa kachikhulupiro kalikonse.

<sup>88</sup> Tsopano kumbukirani, kulungamitsidwa ndi kwa kachikhulupiro, izo nzoona, inu mumakhulupirira kulungamitsidwa monga kwina kwake monga Achilutera ndi aliwonse a masetilayiti awo. Ndicho chimene iwo ali, masetilayiti, koma sananyamukebe pansi panobe. Inu mukatenga kuyeretsedwa ndi masetilayiti awo. Mukuti, “Kodi masetilayiti a Achilutera ndi chiyani?” Chabwino, Mpingo wa Khristu ndi gulu limenelo uko. “Kodi masetilayiti a Wesley ndi chiyani, kwa Amethodisti monga choncho?” Nazarene, Pilgrim Holiness, masetilayiti awo. Ndiyeno Achipentekoste ndi masetilayiti awo, ndege, ndithudi, a umodzi, uwiri, utatu, unayi, zonzezi mpaka mmwamba, Foursquare, Mpingo wa Mulungu, zonse zikadali tizikhulupiro mu chipembedzo.

<sup>89</sup> Koma wa muchombo amaswa chotchinga cha phokoso. Iye amangopitirirabe modutsa. Iye samamva kalikonse. Oh, mai! Iye amangopitirira zonse zimenezo. Mwaona, iye ali mmwamba mmenemo komwe zinthu zonse. . . Iye akukhala mu Kukhalapo kwa Mulungu. Inde, bwana. Iye analonjeza izo, Mawu Ake amanena kuti Iye ndi Wansembe Wamkulu. Inu mukuona choyezera chachikulu chija chakhala kunja uko chikusuntha? Mumuwone Iye mu msonkhano. Inu mukhoza kuyang’ana pamene Mzimu Woyera ukutsika mu mawonekedwe a Lawi

la Moto monga Iye analonjezera. Munthu sakhala pamenepo akuyesera kulingalira Izo ndi sayansi, wokhulupirira weniweni. Kodi Iye ndi chiyani? Iye ndi Sikilini ya Choyezera. Muwoneni Iye. Iye akuyamba kuloza pozungulira. Ameni. Ndipo icho chikumugwira uyo apo, wamuchombo ameneyo. “Iwe uli ndi khansa. Iwe uli ndi *chakuti-ndi-chakuti*. Ndiwe *Chakuti-ndi-chakuti* ukuchokera ku malo akuti. Ambuye Yesu akuchize iwe.” Aleluya! Iye amanyamuka. Amuchombo! Oh, mai, ndi Mpingo wotani umene Iwo ukuyenera kukhala! Uli pano.

<sup>90</sup> Chimene takwanitsa kuchita chatsimikiziridwa ndi sayansi. Iwo anachiwonetsa icho uko pa Chiwonetsero cha Dziko. Ife tiri nacho icho. Ameni. Icho chikutsimikiziridwa konsekonse, m’badwo wa muchombo umene tikukhalamo. Mwaona, “Icho chinapangidwa ndi zinthu zomwe sziwoneka.” Mwaona, icho chinapangidwa ndi chinachake chochokera Kumwamba. Ndi Mulungu Mwiniwake; inu muli mu dera lachisikisi limenero. Ndi mphamvu ya Mulungu. Ife takhala mu malo otero mpaka ife takwezedwera mmwamba kupita ku dera limenero, kupitirira chinthu ichi cha kupita kumanda ndi kumalira, chinthu ichi choyika nkhata pa chotsegulira chitseko ndi kutsazikana ndapita kwanthawizonse. Aleluya! Ife tinalowa muchombo, ndipo tinanyamuka kupita kutali uko ndi kukawona kumene izo ziri, ndipo tinabwereranso. Ulemelero! Ife tikupita Kwathu kuseri kwa thambo kutaliko, kupitirira kulingalira kwa munthu. Momwe okalamba adzasinthidwe mu mphindi ya kuphethira kwa diso. Ife tidzawawona iwo kumeneko, amuna ndi akazi okalamba, ali achicheperenso. “Inu mukudziwa bwanji?” Baibulo limaphunzitsa zimenezo! Ndipo, Mulungu anatumiza chombo mmwamba mmenemo, ife tikudziwa chimene izo zonse ziri, kubwereranso. Palibe kudandaula za kufa. Kufa si kanthu. Ndithudi, ndi kukhala moyo. Inde, bwana. Ndi kungonyamula mapazi anu pansu kuti tizipita. Oh, nzodabwitsa bwanji!

<sup>91</sup> Iye analonjeza zinthu zonsezi mu Mawu Ake, pakuti Ahebri 13:8 amati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Zinthu zimene Iye anali wokhoza, Mulungu akhoza kuzikwaniritsa mwa munthu mmodzi amene angadzipereke yekha kwa izo, ku Mawu a Mulungu, chifukwa, monga ine ndinanena usiku watha, iye nthawizonse ankayima ndi Mawu.

<sup>92</sup> Tsopano, kodi mukudziwa chiyani, wamuchombo kwenikweni si chinthu chatsopano ayi. Nanga bwanji Eliya? Ngati iye sanali wamuchombo, ine sindinamuwonapo mmodzi. Iye anapita kumene John Glenn sanaganizepo zopita.

<sup>93</sup> Chabwino, inu mukudziwa, iwo anali naye mmodzi amene ananyamuka mu kumayenda pang’onopang’ono nthawi yina. Dzina lake anali Enoki. Iye amangoyenda nkumakwera mmwamba, koma iye anali wamuchombo. Ndithudi. Iye anali ndi mpweya wamphamvu, sankasowekera kuti asinthidwe,



palibe. Ayi, iye anali ali kale ndi mpweya wamphamvu pamene anayamba kuyenda. Anangoyenda kumapitirira kuchoka mmagawo onse ndi chirichonse, anayenda kutuluka mu Kukhalapo kwa Mulungu.

<sup>94</sup> Ndipo chotero munthu wina wachikulire anali atatopa ndipo sankakhozanso kuyenda bwino aponso. Iye anali atakangana ndi Yezebeli, ndi tsitsi lake lalifupi ndi penti ndi chirichonse, mpaka Mulungu anangotumiza gareta kumeneko, anati, “Ndingokulola iwe ukwere kudutsa mmitambo masana ano.” Wamuchombo!

<sup>95</sup> Nthawi ina Mmodzi anabwera kudzatifera ife tonse, ndipo Mulungu anamuwukitsa Iye tsiku lachitatu. Ndipo amuna faivi handirede anayima pamenepo ndipo anamuwona Iye akutengedwera mmwamba kukalowa mmitambo, ndi Liwu likuti, “Ine ndidzabweranso.” Ndipo Angelo anabwerera ndipo anati, “Yesu yemweyu amene anatengedwera mmwamba, Wamuchombo Wamkulu, adzabwereranso mwanjira yomweyo, mu mtundu womwewo wa nyumba yomwe Iye alimo, thupi, lachisavundi.” Aleluya! “Ndipo ife tidzakhala ndi thupi ngati thupi Lake Lomwe la ulemelero, pakuti ife tidzamuwona Iye monga Iye aliri.” Oh, aleluya! Iye anathyola zotchinga phokoso zonse, zotchinga kulingalira zonse, ndipo anapita kupyola kulingalira, anapita kudutsa china chirichonse.

<sup>96</sup> Ndipo munthu aliyense amene amukhalira moyo Mulungu adzayenera kupita kudutsa mphamvu zisanu zirizonse, iye adzayenera kuti apite ku maphunziro aliwonse, chirichonse chimene munthu anakwanitsa kuchichita, ndi kumukhulupirira Mulungu, kuswa chirichonse ndi kuchiyika icho pambali, ndi kusesera mmwamba kukalowa Kumwamba. Amen. Oh, chimene amuchombo ndi ena otero akwanitsa kuchita mwachirengedwe, Mulungu wakwanitsa kuchita zimenezo mwa mpingo Wake, mwauzimu, mwa anthu auzimu amene ati akhulupirire. Mwamuna kapena mkazi aliyense amene angayerekeze pa nthawi iliyonse, nthawi iliyonse kuti amutenge Mulungu pa Mawu Ake, ndi wamuchombo.

<sup>97</sup> Iwo adzati, “Oh, izo nzosamveka. Mukuwamva anthu amenewo akulira, akufuula, mukumva zimenezo? Oh, izo nzosamveka konse.” Iwo sakumvetsa.

<sup>98</sup> Winawake anandiuza ine, anati, “Inu munali ndi loto, M’bale Branham, pamene inu munawona malo amenewo.” Ine sindinakhalepo ndi loto. Ine ndinali nditayima pamenepo ndikuyang’ana pansu pamene ine ndinali nditagona pa bedi. Ine mwina ndinali ndikulota pa bedi, koma ine ndinali pamwamba apa ndikudziyang’ana pansu inemwini. Mukuona? Oh, Iye anangondipatsa ine kukwera kwa chombo pang’ono mmawa umenewo, kundiwonetsa ine kumene ndikupita. Ndipo izo zikuwonetsa kuti choyezera chako chidzalozza icho, ndendende kumene izo ziri. Tsopano, si ineyo, ndi Iyeyo. Ndi mzimu

wako mwa iwe ukukhulupirira Uthenga umenewo, ndipo ndi Mzimu Woyera wayima pano pamene ine ndiri, ndipo iwe umakhulupirira izo monga choncho ndipo izo zimalumikizana; ndipo apa izo zimabweretsanso, yankho lako. Wamuchombo! Amen. Oh, nzodabwitsa bwanji! Inde, bwana.

<sup>99</sup> Zopambana, sayansi yachita chinthu chachikulu. Ndipo, inu mukudziwa, iwo azichita izo mopambana kwambiri mpaka iwo akuyamba kudzychitira okha mantha. Uko nkulondola. Iwo ali ndi ukulu wochuluka kwambiri mpaka iwo akudziwopa okha. Inu mukudziwa, iwo ananena kuno pafupifupi zaka ziwiri zapitazo, izo zinali “mphindi zitatu isanafike pakati pausiku.” Iwo akuchita mantha. Kodi iwo akuchita chiyani? Tsopano, munthu wakhala wokhoza, pambuyo pa chirengedwe chake mwa wamuchombo wachirengedwe, tsopano iye wakwanitsa kukhala ndi wamuchombo uyu. Ndipo iye akuganiza tsopano kuti pamene Russia adzayambe kuphulitsa dziko ili, kapena dziko linalo, iye adzanyamuka nkumapita ku mwezi.

<sup>100</sup> Ine ndinawona kanthu kakang’ono kokongola kwambiri tsiku lina, iko kwenikweni kanali kokongola. Apo panali Amwenye awiri aang’ono atayima, akuyankhulana wina ndi mzake, timimba tating’ono, inu mukudziwa, monga choncho, ndi nthenga mmwamba kuseri kwa mitu yawo, ndipo akungogwirana chanza wina ndi mzake, kuisitana wina ndi mzake. Anati, “M’bale, posachedwapa tilitenganso dzikoli kubwerera kwa ife, azungu akupita ku mwezi.” Anati, “Posachedwapa tilitenganso dziko lathu. Mzungu akupita ku mwezi, chotero ife tilitenganso dziko lathu.” Izo ziri bwino.

<sup>101</sup> Oh, tsopano iwo onse akufuna kupanga zochuluka za zitini za amu chombo izi kuti adzathe kulowamo mmenemo. Ndipo a—m’badwo wa atomiki ukubwera, iwo adzaliphulitsa dzikoli, iwo adzangokoka *ichi* ndipo onse nkudzapita ku mwezi, adzakhala ndi ulendo wopita ku mwezi, ndi kukakhala nazo zonsezo, ndipo chotero iwo adzangokazipangira chuma china ku mwezi. Iwo sadzakafika kumeneko. Ine sindikukhulupirira, ndi mtima wanga wonse, iwo adzakafika konse kumeneko. Mukuona?

<sup>102</sup> Koma, pa nthawi yomweyo, wokhulupirira weniweni woona mwa Khristu adzalowa mu Chombo chake. Amen. “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwira mu Chombo chimodzi.” Oh, Thupi limodzi! Icho chikhoza kupirira mphamvu iliyonse. Iwo anayeserapo izo mu ng’anjo ya moto, icho chidzapirira moto, chotero icho sichidzatha kuyaka; kuchulukitsa kaseveni kutentha kwake. Iwo anayeserapo icho mu chirichonse, chimatuluka bwino bwino. Chotero asayansi yauzimu yakwanitsa kutsimikizira kuti akhoza kupirira chirichonse. Chotero a—wokhulupirira weniweni wauzimu wadziperekeza yekha ndipo wakalowa mu Chombo cha Mulungu, Khristu, akukhulupirira zinthu zonse; kuika pambali tizikhulupiriro take, tizikhulupiriro ta Chipentekoste, tizikhulupiriro ta

Baptisti, tizikhulupiriro ta Methodisti. Iye wangolowa mu Chombo, akuti, “Ambuye, icho chikonzeka liti?” Oh, mai! Kodi iye akuchita chiyani? Iye akubwera ku misonkhano yaying’ono, iye akumvetsera ku kuwerenga chotsitsa kwa Mawu a Mulungu.

<sup>103</sup> Inu mukudziwa, pamene John Glenn anakhala pamenepo mmawa umenewo, iwo anali akumvetsera ku kuwerenga chotsitsa. “Teni, naini, eyiti, seveni, sikisi, faivi, foro, firii, thuu, wani, ziro.” Mukuona? Ndipo tsopano iye wafika pamalo amene akuti, “Kwatsala mphindi zitatu kuti chinachake chinyamuke.” Iwo sakudziwa chimene icho chiri. “Mphindi zitatu kuti tikhale ndi ola la ziro.”

<sup>104</sup> Tsopano zindikirani, wokhulupirira weniweni amakhala mwa Khristu. Palibe kutsutsidwa kwa iwo amene ali mwa Khristu. Amalalikirira Mawu, amakhala ndi Mawu. Ine sindikusamala chimene zipembedzo zikunena, iwo awakhulupirira Iwo. Iwo adzayima pomwe apo, chifukwa iwo ndi Mawu. Zipembedzo zimayambitsa mkangano waukulu ndi kuwachotsa iwo, kuwathamangitsa iwo, ndi kunena kuti “iwo ndi openga,” chirichonse monga choncho. Koma iwo amakhalabe ndi Mawu amenewo. Bola ngati Mulungu analonjeza zimenezo, iwo amakhala pamenepo chifukwa iwo ndi amuchombo. Iwo amakhulupirira Mawu. Ndipo palibe njira yowachotsera iwo. Iwo adzakusiyani inu mulimonse, chotero basi—ingowasiyani iwo okha kanthawi.

<sup>105</sup> Koma iwo ali mmenemo, atakhala mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu, akumvetsera ku kuwerenga chotsitsa, *Mibadwo Ya Mpingo* ndi zina zotero. Ulemelero! Zimakupangitsani inu kumverera bwino, sichoncho izo? Kumvetsera ku kuwerenga chotsitsa! Kuwerenga chotsitsa ndi chiyani? “Zinthu zonsezi zinalonjezedwa, apa ndi pamene izo zinadzachitika. Zinthu zonsezi zinalonjezedwa, apa ndi pamene izo zikuchitika. Kumene kuli lonjezo, apa ndi pamene izo zinachitika. Zokwanitsa kuchita zimene Iye walonjeza lero, ndi izi apa pakati pathu pomwe.” Kodi iwo akuchita chiyani? Akumvetsera ku kuwerenga chotsitsa. Izo zafika patali bwanji? Njira yonse kuchokera kwa Lutera. Kuwerengera chotsitsa! “Kulungamitsidwa, kuyeretsewa. . . Teni, naini, eyiti, seveni, sikisi, faivi, foro, firii, thuu. . . Kumakwera mmwamba!” Kodi iwo akuchita chiyani? Akudikirira kunyamuka, ora la ziro. Amen.

[M’bale Branham, maora eyiti kenako, anadzajambula gawo lomalizira lowonjezera ili limene linadzayikidwa apa ngati ndime 106-111. Iye anadzazifotokoza izi pa ulaliki wake wamadzulo, *Mu Kukhalapo Kwake*, ndime 4-5—Mkonzi].

<sup>106</sup> Kuzungulira kwakukulu uku kumene Mpingo ukukonzekera kuchita, ndi nthawi yayikulu ya kuwerenga chotsitsa, Ndikufuna ndikufotokozereni chimene ndikuganiza kuti

kuwerengera chotsitsa kuli. Tsopano, ine ndikuganiza ife tangodutsa mu izo kumene mu mpingo muno. Ndipo tsopano inu mukuzindikira kuti, pamene wamu chombo wachirengedwe akukonzekera kuchoka pa dziko lapansi, pamakhala kuwerengera chotsitsa kuyambira pa teni kubwerera mpaka ziro. Tsopano, ine sindinayesere kuwuswa Uthenga uwu ndi kuwupatsa iwo mafotokozedwe auzimu, chifukwa izo zingatenge nthawi yochuluka kwambiri mmawa uno. Koma ine ndikufuna kuti ndiyesere kufotokoza ichi kwa inu, kuti *teni* ndi nambala ya “chidziko,” munthu. Koma *seveni* ndi nambala ya “Ungwiro wa Mulungu.” Masiku sikisi Iye analenga miyamba ndi dziko lapansi, ndipo lachiseveni Iye anadzapuma. Ndipo zaka sikisi sauzande dziko likuyenera kuvutika motsutsana ndi tchimo, kapena mpingo uvutika motsutsana ndi tchimo, ndipo la chiseveni ndi Zakachikwi, Sabata.

<sup>107</sup> Seveni ndi nambala yangwiro ya Mulungu. Ndipo tsopano Iye watipatsa ife kuwerengera chotsitsa kolondola, ndipo kuwerengera chotsitsa Kwake si teni, koma seveni. Ife tangodutsa kumene mu izo mu *Mibadwo Isanu Ndi Iwiri Ya Mpingo*. Tsopano ife tikupeza, ndipo uko mu Chivumbulutso, kuwerenga chotsitsa koyamba kunali mu m’badwo woyamba. Kuwerenga chotsitsa kwachiwiri, m’badwo wachiwiri. Ndipo mpaka kuwerenga chotsitsa kwa chiseveni. Ndipo apa zikuwoneka patsogolo pathu, monga chithunzi ichi chajambulidwa, kuti ife tinali ndi kuwerengera chotsitsa uku. Nambala yoyamba kuwerengedwa inali Efeso. Nambala yachiwiri kuwerengedwa inali Smurna, Smurna. Kenako Pergamo. Tiyatira. Yachisanu inali Sarde. Yachisikisi inali Filadelfia. Ndipo yachiseveni inali Laodikaya, m’badwo wa mpingo wotsiriza. Kenako ndi nthawi ya ziro, kuti Mpingo uzinyamuka, mibadwo ya mpingo itatha kutumikira nthawi yawo. Tsopano, ife tikudziwa m’badwo wa Tiyatira unabwera ndipo unapita, ndipo m’badwo wa Aefeso unabwera ndipo unapita, m’badwo wa Filadelfia unabwera ndipo unapita. Ndipo ife tiri mu m’badwo wa mpingo wachiseveni, pa mapeto ake, m’badwo wa Laodikaya. Ndipo kumeneko ndiko kuwerenga chotsitsa.

<sup>108</sup> Ngati inu mungazindikire mu maphunziro athu ammbuyomu a mpingo, Iye ananyamula mdzanja Lake *nyenyezi seveni*, zimene ife tinazipeza kuti ndi “atumiki seveni a mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo.” Aliyense wa iwo akuzindikiritsidwa mwangwiro pamene Mulungu amatenga kuwerenga chotsitsa Kwake. Kuyambira nthawi imene Iye anadzachoka, mpaka nthawi imene Iye adzabwerenso, Iye akusonkhanitsa anthu chifukwa cha Dzina Lake. Zinayambira pa Tsiku la Pentekoste. Woyamba, mpingo wa ku Efeso, nyenyezi ndi wamthenga wa mpingo umenewo ife timakhulupirira kuti ndi Paulo Woyera. Iye wabwera, ndipo nambala wani yawerengedwa. M’badwo wa

mpingo wachiwiri, umene uli Smurna, anali Ireniasi, woyera wamkulu wa Mulungu amene anatsogolera m'badwo wa mpingo umenewo pamapeto. M'badwo wa mpingo wachitatu, umene unali Pergamo, anali Kolamba Woyera amene anali woyera wamkulu wa Mulungu. Mu nthawi ya M'badwo wa Mdimba, mu mazunzo, m'badwo wachinayi ndi kuwerenga kwachinayi, Martin Woyera waku Tours, woyera wamkulu akubwera kuchokera ku France. M'badwo wa mpingo wachisanu, ndipo mtumiki wake anali Martin Luther pa kuwerengera chotsitsa. M'badwo wachisikisi anali John Wesley pa kuwerenga chotsitsa.

<sup>109</sup> Tsopano ife tiri mu m'badwo wachiseveni, m'badwo wa mpingo wa Laodikaya. Ndipo tikumufunafuna mtumiki wamkulu umeneyo wa kuwonekera kwachiwiri kwa Eliya, pa kuwerenga chotsitsa. Ndipo mwamsanga pamene iye adzawonekere, ndiye ndi nthawi ya ziro ndipo Mpingo udzayamba kumapita Kwawo, udzatulukira kumapita mu mlengalenga, kupita Mmiyamba, kumapitirira kudutsa mwezi, nyenyezi, china chirichonse, ndi kukakomana ndi Yesu.

<sup>110</sup> Kodi izi zinachokera kuti ndipo iwo anapita kuti? Mu Chombo ichi. Kodi anthu ankalowa chotani mu Chombo poyamba? Umo ndi momwe iwo adzayenera kulowamo mu icho malo aliwonse, nthawi iliyonse. Uko nkulondola. Ayenera kudzabwera mwanjira yomweyo imene oyamba anachitira, chifukwa kuzungulira kwakukulu uku kwa thupi lalikulu la anthu. Kutu mu nthawi ya Nowa, panali khomo limodzi lokha, ndipo khomo limenero linali khomo lokhalo lolowera. Chirichonse chimene chinadzalowa, ziribe kanthu kuti iwo anapita mu chipinda choyamba pansu pa kulungamitsidwa, chipinda chachiwiri, kapena chipinda chachitatu, iwo onse analowera khomo limodzi. Iwo onse anadzabwera mwanjira yofanana.

<sup>111</sup> Ndipo ndi chinthu chomwecho mu tsiku lino la chombo. Ife tiyenera kubwera mwanjira yomweyo, kubwera mwanjira yomweyo, mwa Uthenga womwewo, mwa Khristu yemweyo, mwa Mphamvu yomweyo imene iwo anailandira pa Tsiku la Pentekoste. Mwanjira yomweyo! Izo zakhala nthawi zonse ziri Mmodzi yemweyo, chifukwa Ilo ndi Khomo lomwelo. Ndipo kodi ife timalowa bwanji mu thupi ili? Polowera Pakhomo. Ndipo Yesu ndi Khomo ku Thupi ili. Chotero ife timalowa mkati ndipo timabadwira mu Ufumu wa Mulungu, kudzera pa Khomo, Yesu Khristu. Ndipo tsopano Khomo latsala pang'ono kutseka ku Laodikaya, kuwerengera chotsitsa komaliza, ndipo Mpingo ukukonzekera kutenga kuzungulira kwake pamwamba pa zisautso zonse, chirichonse, ndi kuwulukira ulendo wake kukalowa mmiyamba ya Mmiyamba, kuwutengera Mpingo ku chifuwa cha Mulungu. Amen. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Amen.

<sup>112</sup> Mmawa pamene John... Glenn uyu ananyamuka kumusi

uko, aliyense anali pa nkhope zawo, akulira ndi kupemphera, akudabwa chimene iye akanati akwaniritse. Ndipo chinthu choyamba, moto unayamba kufalikira kuchokera ku ma atomu amenewo pamene mzinga wawukulu uwo unanyamuka uko ku Cape Canaveral, ukupita mmwamba mlengalenga monga choncho, ndipo anthu akukuwa ndi kulira ndi kudabwa chimene chingachitike kwa wamu chombo wawo amene ankapita mmwamba.

<sup>113</sup> Oh, koma Mpingo, ulemelero, iwo ukumwaza moto nawonso. Amen! Kuweringa chotsitsa kukubwera! Amen! “Kulungamitsidwa, kuyeretsewa, ubatizo wa Mzimu Woyera, m’badwo pa mpingo wa Laodikaya,” ife tiri kumapeto! Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Vuto ndi chiyani? “Teni, naini, eyiti, seveni, sikisi, faivi, foro, firii, thuu...ziro!” Iwo sadzakhala akulira, koma padzakhala kuyimba ndi kufuula ndi kutamanda Mulungu, pamene Mpingo ukutenga kusuntha kwake kwa mu chombo kupita mlengalenga kukakhala ndi Yesu Khristu. Amen.

<sup>114</sup> Mu zokwanitsa kuchita za zachirengedwe, iwo ananyamuka kupita ku mwezi. Mu zokwanitsa kuchita zauzimu tikunyamuka kupita Kumwamba. Amen! Wamu chombo wachirengedwe akuyesera kuti amupezere iye malo ku mwezi. Ife tiri ndi malo kale Kumwamba okonzeka. “Mu Nyumba ya Atate Anga muli nyumba zambiri. Ine ndikupita ndi kukakukonzerani inu malo, ndi kudzatumiza Wamuchombo kuti adzakutengeni inu.” Kuweringera chotsitsa kwayambika! Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Amen. Kuweringa chotsitsa! “Teni, naini, eyiti, seveni, sikisi, faivi, foro, firii, thuu, wani, ziro!” Moto wayamba kufalikira, utumiki wavekedwa korona mu Ulemelero. Aleluya! Ndipo chombo chakalecho chayamba kunyamuka, osati kuloza ku mwezi, koma kuloza ku Ulemelero. Kutaliko icho chiri, moto wa Mulungu ukufalikira. Mphamvu ya Mzimu Woyera ikumukweza iye mmwamba ndi kudutsa ku mwezi, nyenyezi, kudutsa chirichonse chimene munthu angachikwaniritse. Mpingo udzawulukira ku zifuwa za Mulungu Kumwamba, umodzi wa mmawa uwu. Abwenzi, munthu watha kukwaniritsa chimene ali nacho ndi zinthu zawo zachirengedwe, ndipo Mulungu (ine ndatsimikizira izo apa) wazifanizitsa izo mwauzimu.

<sup>115</sup> Tiyeni tilowe mu Chombo, mwamsanga! Zitseko zitsekedwa pakapita kanthawi. Kuweringa chotsitsa kwayambika! Sayansi imati kuweringa chotsitsa kwawo ndi maminiti atatu. Kwathu kukhoza kukhala patsogolo pa izo, zikhoza kukhala “wani” kukonzekera “ziro!” Tiyeni tilowemo. Kodi mukukhulupirira kuti kuweringera chotsitsa kwayambika? Tiyeni tiweramitse mitu yathu ndiye mphindi yokha.

<sup>116</sup> Atate! “Teni, naini, eyiti, seveni, sikisi, faivi, foro, firii, thuu...” Mulungu! “Mafuko akusweka. Israeli akuwuka,

zizindikiro zimene aneneri ananenera; masiku a Amitundu owerengeka, ndi zowopsya zochuluka; bwererani, O omwazika, kwanu.” Ndi tsiku lotani! Kuwala kwamadzulo kukuwala. O Mulungu, ife tikupemphera kuti wosakhulupirira aliyense mwaliwiro ayike pambali malingaliro ake onse a maphunziro, malingaliro ake onse amene ali osiyana ndi Mawu Anu, ndipo mmawa uno alowe mu Chombo chaulemelo ichi, chifukwa ife tinabadwira mwa Iwo, mmenemo kuti tidzakhale gawo la wa Muchombo.

117 Ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, ndi mu Thupi la Khristu lalikulu ili, kuti Inu muwabatize okhulupirira lero ndi Mzimu Woyera. Mulole dziwe lidzaze ndi anthu mmawa uno, akuvomereza machimo awo ndi kuyikidwa mmanda mu Dzina la Yesu Khristu, ndi kumakwera Chombo chakale, Ambuye, chimene chikupita kuwudutsa mwezi ndi nyenyezi, ndi kumapita kudutsa tizikhulupiriro, zipembedzo. Ife tinawerengera chotsitsa kale. Inu munatiuza ife chimene chikanati chidzakhale, atatu, magawo atatu awa a ichi. Inu mwanena za mibadwo ya mpingo, momwe iyo idzapitire, m’badwo wa mpingo woyamba, m’badwo wa mpingo wachiwiri, m’badwo wa mpingo wachitatu, wachinayi, wachisanu, wachisikisi. Kuwerenga uku ndi seveni. Ndipo utatha wa seveni, m’badwo uno; ife tiri kale mmenemo, m’badwo wa mpingo wotsiriza. Ndipo tsopano kuwerenga chotsitsa kukupitirira. Mibadwo yawerengedwa kale, m’badwo wa Chilutera, m’badwo wa Wesley, m’badwo wa Pentekoste. Ndipo tsopano, Ambuye, kusonkhanira mu Chombo, ndi galasi lokulitsa lalikulu patsogolo Pake, ife tikukhoza kuwona Ulemelero, kumuwona Yesu, kumuwona Iye mu mphamvu Zake zonse, kumuwona Iye mu malonjezo Ake onse. Chirichonse chimene Iye analonjeza chikunyezimira pa ife. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha izi.

118 Mulungu, mulole mpingo lero ulowe mwamsanga mmalo otetezeka, pakuti posachedwapa pakubwera ora la ziro ndipo chitseko cha Chombo chachikulucho chidzatsekedwa, ndege ya Chombo. Ndipo ife tidzapita monga Nowa anachitira pamene iye analowa mu chombo chake, monga izo zinali, iye anayandama ndi pamwamba pa madzi onse a chiweruzo. Ndipo, Atate, ife tikufuna kuti tilowe mwa Inu kuti ife tidzathe kuyandama kudutsa mitsinje ya nthawi, kudzadutsa Mars, Jupiter, Venus, mpaka ku Njira-Yoyera ngati Mkaka, kupitirira ndi kupitirira ndi kupitirira, kumene wamu chombo wachirengedwe sadzadziwa kanthu za izo. Koma ife tikuwona kuti Inu mukumulola iye kuti achite izo mwa chizindikiro, kuti ife tidzathe kukhala okonzeka kuti tizipita. Tikuyenda kuchokera padziko lapansi. Perekani izi, Ambuye. Kudzera mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikupempha izi.

119 Apa pali mipango, Ambuye, ili apa, imene anthu odwala atumiza. Iwo akukhulupirira, Ambuye. Ndipo mulole iwo

akhale mamembala athunthu amuchombo mmawa uno. Mulole mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse Yemwe amanyezimiritsa Baibulo Lake pa izi, zimene ankazichotsa pa thupi la Paulo Woyera, mipango ndi zovala, ndipo odwala ndi osautsika ankachiritsidwa. Mulole wokhulupirira wa muchombo uyo, pamene izo zikamukhudze iye, akanyamuke, Ambuye. Matenda kumbuyo! Mulole munthu wodwala aliyense pano pakali pano, Ambuye, alowe mwa Khristu Yesu, ku Mawu Ake, lonjezo Lake. Ndi kumati, “Apempheni Atate chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho.” Mulole iwo ayambe kuwerengera, “Teni, naini, eyiti, seveni, sikisi, faivi, foro, firii, thuu... ziro. Kunyamuka, Ambuye!” Mulole iwo awuke kuchokera mu zikuku, machira, chirichonse chimene chingakhale. Mulole iwo adzuke ku matenda awo omangika, kuti azipita kutali uko mu danga lakunja kumene sayansi ya madokotala, palibe mmodzi wa iwo, amadziwa kalikonse za izo, kumene Mphamvu ya Mulungu inalonjeza mwa kafukufuku wa sayansi ya Baibulo pano, kapena kafukufuku wauzimu, kani, wa Baibulo; kukasonyeza kuti Mulungu wakhala ali Mulungu, akadali Mulungu, Iye adzakhala nthawizonse Mulungu, ndipo Iye ndi Wopandamalire, Wamphamvu, Wamphamvuzonse, Wopezekaponseponse Uyo amene angathe kusunga Mawu Ake; ndipo akhoza kuchita zinthu zonse, ndipo anatilonjeza ife kuti zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene ati adzakhulupirire. Mulungu, perekani zimenezo.

<sup>120</sup> Mulole mwamuna wopulupudza uja kapena akazi, mnyamata kapena mtsikana, mmawa uno, amene sali mmenemo kumvetsera ku kuwerenga chotsitsa kwa Mawu a Mulungu, podziwa kuti ife tiri pansu pomwe, tawerenga chinthu chotsiriza. Iye wakonzeka kufuula “ziro” pa nthawi iliyonse, ndipo kuti mpingo uzipita. Ife tikuwona Uthenga ukutha. Ife tikuwona chizunzo chikukwera, monga ife tinakambira usiku watha. Ife tikudziwa kuti nthawi yayandikira. Kuwerenga chotsitsa kwatha. Inu mwatithandiza ife pano pa nsanja kuti tiyibweretse kubadwo ya mpingo apa, ndi kutenga china chirichonse ndi kutimikizira izo, kuti pakali pano nthawi iliyonse izo zikhoza kuchitika. Mulungu Wamphamvuzonse, Amene munalenga Miyamba ndi dziko lapansi, mutumize zifundo Zanu kwa anthu ndipo mupereke kwa iwo icho chimene Inu mwawasungira iwo. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu.

<sup>121</sup> Ndipo mwamuna ndi mkazi aliyense ndi mutu wawo woweramitsidwa. Ngati pali ena pano amene sakumudziwa Khristu ngati Mpulumutsi wawo mmawa uno, ndipo mukufuna kuti mumudziwe Iye ndi kulowa mu chikhaliidwe cha Wamuchombo ichi cha chisomo cha Mulungu, kupita mu Mkwatulo, mungakweze dzanja lanu ndi kuti, “Ine ndi wokonzeka, ndikufuna kukonzekera Mkwatulo, M’bale Branham. Ndipemphereni ine.” Mulungu akudalitseni



inu. Mulungu akudalitseni inu, inu. Mulungu akudalitseni inu, ndi inu. Kunja, mkati, kulikonse kumene inu muli, mungokweza dzanja lanu. Mwa ichi, nenani, “Mulungu, ndilowetseni ine.” Mulungu akudalitseni inu. “Ndikufuna kumva kuwerenga chotsitsa. Ndikufuna kumva iko. Ndikufuna ndizikhala ndikudziwa kuti ndine wotetezeka, kuti pamene moto uzidzayaka sindidzakhala pansi pano mu kavalo ndi ngolo. Ine sindidzakhala ndiri mu tchalitchi, ndikukwera mu galimoto. Sindidzakhala mu imodzi imene idzangonyamula mapazi ake pansi tsopano, kungokwanitsa kulumphu ndi kudzakhala ndi phokoso lambiri. Ndikufuna ndidzakhale mu chinachake chimene chidzanditengere kudutsa mwezi ndi nyenyezi. Ine ndikufuna ndizimvetsera ku kuwerenga chotsitsa; osati kachikhulupiro kena, bungwe lina. Koma ndikufuna ndidzakhale mwa Khristu, kumene ndidzakhaze kuyenda kudutsa chirichonse chimene chiri chifukwa pakati pa anthu. Ndikufuna ndidzapite.”

<sup>122</sup> Kodi pali wina tisanapemphere? Alipo...? Mulungu akudalitseni inu, dona wamng’ono. Mulungu akudalitseni inu, mnyamata. Mulungu akudalitseni inu, ndi inu kumbuyo uko. Ine ndikuwona dzanja lanu, ndipo Mulungu akuliwona ilo ndithudi. Ndi inu, m’bale wanga, inu m’bale. “Ndikufuna ndikhale mu kuwerenga chotsitsa. Mulungu, ndiloleni ine ndiike pambali cholemetsa chirichonse.” Mulungu akudalitseni inu, m’bale. “Ine ndikufuna kuyika pambali tchimo lirilonse. Ine ndiri ndi kupsya mtima M’bale Branham. Oh, ine sindingalowe mu Icho monga choncho. Ndikupemphera Mulungu kuti andichotsere izo. Ine—ine, M’bale Branham, ine—ine ndimamwa pang’ono. Sindikufuna ndizichita zimenezo. Pempherani kuti ndiyike izo pambali. Ine ndimasuta. Sindikufuna ndizichita zimenezo. Mulungu akudziwa kuti sindikufuna ndizichita zimenezo. Chinthucho chimangondipangitsa ine kumangidwa, ine—ine ndimangochita icho, ndikumalephera kuchoka kwa icho. Ndikudziwa kuti izo ndi zolakwika, ndipo sindikuyenera kumachita izo. Ine sinditero! Chinthu china, ine ndakhala ndikukayikira Mawu. Ndakhala ndikudabwa ngati Iwo anali owona kwenikweni. Ndithandizeni ine, Mulungu. Ndiloleni ine, ndiloleni ine ndizingokumbukira kuti zonse za Iwo ndi zoono, ndipo ine ndikukhulupirira Iwo. Ndikufuna ndizimvetsera ku kuwerenga chotsitsa. Ndikufuna kukhala pamalo amene nthawi iliyonse ndiziwona Mawu a Mulungu akunena chirichonse, ine ndikufuna ndizivomereza izo ndi ‘ameni’ ndi kunena kuti ‘Ndi Inu, Ambuye.’” Tsopano nonse... Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, aliyense wa inu.

<sup>123</sup> Kodi alipo ena pano amene akudwala, ndipo akuti, “M’bale Branham, mmawa uno ndine Mkristu, koma ndine... Ine ndakhala... ndinalandira Mzimu Woyera. Ndatsika ndege tsopano, ndakonzekera kuwerenga chotsitsa. Ine ndatuluka

mu mitundu yonse ya zipembedzo ndi china chirichonse, ndikumvetsera ku kuwerenga chotsitsa. Koma tsopano ine ndikufuna ndinene chinthu chimodzi ichi, M'bale Branham, mmawa uno, ine ndikudwala. Ine ndiri ndi ntchito yina yoti ndiwachitire Ambuye. Ine ndikumvetsera ku kuwerenga chotsitsa, koma ndikufuna ku—ndikufuna kukhala bwino. Ine ndikudutsa pa izo mmawa uno, ndikumvetsera ku kuwerenga chotsitsa.” Kuwerenga chotsitsa ndi chiyani? Mawu a Mulungu. Akuwerengedwa mpaka pansi. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. “Ine ndikufuna kuti ndimumve Iye ngati Mchiritsi wanga mmawa uno. Ine ndikufuna kukweza dzanja langa ndi kunena, ‘Ndipempherereni ine, M'bale Branham.’” Mulungu akudalitseni inu. Lowani mkati tsopano. Lowani mkati momwe. Paguwapa padzaza, ndi pozungulira pano, awunjikana pansi. Ife sititha kuyendetsa mzere wa pemphero. Iwo ayima mozungulira makoma ndi chirichonse. Ife tangokhala ndi chisokonezo. Ife sitikuyenera kuchita zimenezo. Inu muli mu—inu muli mu. . . Ndinu wa muchombo.

<sup>124</sup> Inu ndi wa muchombo. Inu mukupita kudutsa Luther. Luther samakhulupirira mu izo zonse. Wesley ankasanjika manja. Achipentekoste ankadzoza mafuta. Ndinu wa muchombo, mwapita kupitirira kulingalira kulikonse. Basi chifukwa Mawu ananena chomwecho, ine ndikupitirira. Chabwino, inu mukuti, “Kodi Luther sanakhulupirire? Kodi amenewo sanali Mawu?” Eya, koma Wesley anapitirira pamwamba pake. “Chabwino, Wesley anadzedwa ndi mafuta kapena chinachake. Kodi inu simukukhulupirira izo?” Inde, ndiko kulondola. “Achipentekoste amatulutsa ziwanda.” Eya. “Amayika manja pamenepo, amakhala ndi machiritso mmanja ndi china chirichonse.” Eya, ndikudziwa kuti ndi zolondola, koma zipitirirani. Pitirirani! Wesley samayang’ana mmbuyo kwa Luther, Pentekoste simayang’ana mmbuyo kwa Wesley. Ngakhalenso ife sitiyang’ana mmbuyo kwa Pentekoste. Ndife a muchombo. Ife tapitirira zimenezo. Tiyeni tipitirire. Khristu ananena chomwecho!

<sup>125</sup> Kodi mumachita izo motani? “Bwerani mudzayike manja Anu pa mwana wanga wamkazi ndipo iye akhala bwino,” anatero Myudayo. Yesu anapita ndipo anakamuchitira iye zimenezo, ndiko kulondola. Koma pamene izo zinafika kwa Wachiroma, wa muchombo, iye anati, “Sindine woyenera kuti Inu mubwere pansi pa denga langa. Mungonena Mawu, Ambuye.” Ndipo Iye wanena kale izo. Ndi zimenezotu.

<sup>126</sup> Tsopano tiyeni tikweze yathu—mitima yathu kwa Mulungu. Tiyeni tikweze manja athu kwa Mulungu, mitima yathu kwa Mulungu. Pakuti chirichonse chimene inu mukuchifuna, chipulumutso, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, machiritso Auzimu, chirichonse chimene icho chiri, kwezani manja anu mmwamba ndipo mugwire mtima wanu mu

Kukhalapo kwa Mulungu, ndipo muzindikire kuti mukukhala mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu, ndipo ndinu wa muchombo wa Chikhulupiriro chimenecho. Chiyani? Apa pakubwera kuwerenga! “Teni, naini, eyiti, seveni, sikisi, faivi, foro, firii, thu. . .” O Yesu, kazibwerani tsopano! Ife tikuyika mphamvu ya Dzina Lake. Ndipo monga ife tinawonera usiku watha, Paulo anamukantha munthu ndi khungu, kumulola wina kuti amuponde iye. Ndipo ife tikuwona kuti Yesu akanatha kupanga chirichonse chimene Iye—Iye anachita, mitundu yonse ya zozizwitsa, ndipo komabe anali pa mapeto pomwe a ulendo Wake, poona kuti Iye anamenyedwa ndi kulavuliridwa, ndi china chirichonse. Anthu sanazimvetse zimenezo. Iwo amazindikira kuti Mulungu amachita izo kuti atsimikizire kuti izo ndi zolondola, ndipo kenako amayesa chikhulupiriro cha anthu.

<sup>127</sup> Ambuye, ife tayima pano ndipo tikuona akhungu kwathunthu akulandira kupenya kwawo, matenda; makhansa amene anali mthunzi wa anthu, akuchiritsidwa. Ife tawawona iwo amene anali akufa ndi kugonekedwa kwa maola pambuyo pa maola, ndipo akubwerera ku moyo kachiwiri. Ife tikudziwa kuti ndi—ndi Khristu wathu wamkulu amene ife tiri wa muchombo mu thupi Lake. Ndipo tsopano kuwerenga chotsitsa kwayambika, ndipo ife tikhulupirira mmawa uno chifukwa cha machiritso athu, kwa chipulumutso chatu, ndi kwa chirichonse chimene ife tikuchisowa. Chifukwa pamene ife tipempha izo mu Dzina la Yesu Khristu, Iye analonjeza, “Apempheni Atate Anga chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho.” Ndipo ndizo zonse zimene ife tikuzisowa kuti tichite tsopano ndi kutchula Dzina Lake, ndipo izo zikuyenera kuchitidwa. Ife tikumvetsera kuwerenga chotsitsa.

<sup>128</sup> Ambuye, ena a iwo amene akhala ali ochimwa, anakweza mmwamba manja awo. Iwo akudikirira kuwerenga chotsitsa, pamene pati padzabwere kusinthika mu mtima wawo, izo zidzachotsamo chivundi chonse choyipa chakale. Pali ambiri amene amasuta ndudu, amene ali okonzeka kuti azisiye izo. Ambiri amene achita zinthu zimene iwo samayenera kuchita, ndipo iwo ndi okonzeka kuti azisiye izo, chifukwa ife tikumupempha Mulungu Wamphamvuzonse mu Dzina la Yesu Khristu kuti achotse chirichonse chimene chikutchinga Mpingo mmawa uno, kuchoka ku matenda mpaka ku tchimo, ndi kulola mpingo uno ukhale waufulu. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole mphamvu ndi Mphamvu ya Uthenga waukulu, Moto wa Mzimu Woyera uyambe kumwazikana, ndipo a muchombo aakulu a Mulungu anyamuke kupita ku chokhumba cha mtima wawo lero. Perekani izi, Mulungu Wamphamvuzonse. Iwo ndi Anu. Ndipo mulole iwo alandire machiritso awo, chipulumutso chawo, ndi chirichonse chimene iwo akuchisowa. Ine ndikuwafikitsa iwo kwa Inu, ndipo ndikuwapereka iwo kwa Inu pogwiritsa ntchito pemphero langa, pa guwa pamene Magazi a Yesu Khristu

akukhala atsopano mmawa uno. Mu Dzina la Yesu Khristu mulole iwo alandire chimene iwo akupempha.

Ndipo anthu anati, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi].

<sup>129</sup> Chotero, khulupirani Izo! Izo zikhale chomwecho! Ine ndikuzikhulupirira Izo. Ine ndikukhulupirira. Ameni. Ine ndikudziwa kuti Iye ndi Mulungu. Ine ndikudziwa kuti ndife okonzekera chokwaniritsa chachikulu cha Mulungu. Kodi chokwaniritsa Chake ndi chiyani? Kuchoka pa dziko lapansi. Wa muchombo amapita ku mwezi, dziko lina. Ndipo Mpingo wa Mulungu (kuchokera ku ndege, kuchokera pa nsana wa kavalo ndi zina zotero) ukunyamuka ngati chombo, ukupita ku dziko lina, lomwe liri Kumwamba. Kuwerenga chotsitsa, kukupitirira. Ameni.

Inu mumamukonda Iye? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndiye tiyeni tikweze manja athu ndipo tiyimbe.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye  
Chifukwa Iye anayamba . . .

Chabwino, M'bale Neville.

Ambuye alemekezeke! Ndipo Mulungu akudalitseni inu mpaka usikuuno pamene ine nditi ndikuwoneni inu. 

62-0909M Kuwerenga Chotsitsa  
Branham Tabernacle  
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)